

UNGIWIRO



Zikomo inu, M'bale Neville. Mmawa wabwino, abwenzi. Wokondwa kudzakhala pano mmawa uno, ndipo ine ndikhoza kupereka ndemanga yomweyo pa m'bale wathu. Ine ndinamulonjeza iye kuti ndikhala mowulutsira mawu, ndipo ine—ine ndinaphonya izo sabata imodzi, ndipo sabata yotsatirayo ndinaiwala izo. Chotero ine ndinaganiza kuti nthawi yachitatu ikuyenera kukhala a—nthawi yeniyeni, ndiyenera kuchita izo.

² Chotero ine ndinali kumeneko, mu miniti imodzi ya nthawi, miniti imodzi yokha. Ndipo M'bale Snyder anali panja, chotero ife tinazembera mkati mwachangu kwenikweni, ndipo—ndipo potsiriza tinadzalowa mowulutsira mawu. Ndipo ine ndikuganiza ife tinawasokoneza iwo, ndi chimene ife tinachita, pamene tinadzabwera monga choncho, basi pang'ono chabe. Chotero. . .

³ Ndipo apa ine ndinali, ndikubwera kumeneko, ndimaganiza za phunziro loti ndidzalalikirepo, inu mukudziwa. Ndipo kawirikawiri za ine, zimanditengera pafupifupi ora ndi theka. Ndipo ndiri ndi pafupifupi fifitini, maminiti eyitini a izo nditayamba kale, ndiyeno ndinayang'ana mmwamba, ndipo wotchi inati ndi nthawi yoti tizipita. Chotero ife tidzapitiriza Loweluka likubwerali, kapena nthawiyina. Uko nkulondola.

⁴ Lamlungu lapitali, ife tinali pa mutu wa 10 wa Ahebri, ndipo tinayambira pa ndime ya 1, ndipo sitinapitirirenso.

⁵ Musaiwale misonkhano ku Indianapolis sabata ino. Ngati aliyense wa inu, kapena muli ndi azimzanu kumeneko, bwanji, alembereni ndipo muwauze iwo. Misonkhanoyo idzayamba mawa usiku seveni koloko, ku Cadle Tabernacle mu Indianapolis. Ndipo kukakhala malo okhalako ambiri, pafupifupi anthu leveni sauzande akhoza—akhoza kukhalamo. Ndipo iwo ndi msonkhano wawung'ono, ndi—ndi bungwe laling'ono. Ine sindikudziwa nkomwe kwenikweni kuti dzina la bungwelo ndi chiyani. Iwo ali ndi a—msonkhano kumeneko, kapena msonkhano waukulu.

⁶ Ndipo mu msonkhano umenewu iwo anandifunsa ine kuti ndidzakhale wodzayankhula usiku. Chotero a...ine ndikuganiza chiyanjanocho pachokha, mpingo, bungwelo, ali nawo basi kwambiri, mamembala apang'ono kwambiri. Ndipo chotero. . . Ndiyeno, usiku, ine ndiri—ndizikayankhula pa msonkhanowo usiku uliwonse, Lolemba mpaka Lachisanu. Lachisanu usiku lidzakhala kumalizitsa kwa msonkhano. Chotero, inu muli ndi azimzanu kuzungulira Indianapolis, bwanji, mudzabwere nawo.

⁷ Ndipo pa twente-firii, mmawa wa pa twente-firii, ngati pangadzapezeke winawake akuyenda kudutsa kuno, basi pa tchuthi chanu; monga uli mwezi wa tchuthi, kawirikawiri, Juni. Minneapolis, a Christian Business Men Internationally adzakhala ndi msonkhano wawo ku Minneapolis. Ndipo msonkhano wa aliyense ndi wa pa twente-firii, kadzutsa. Kadzutsa wa mmawa ndi pa twente-firii Juni. Ine ndikuyenera kukayankhula pa kadzutsa wa mmawa, msonkhano wotsegulira.

⁸ Kenako, pa twente-foro, ndidzakhala ndikadali ku Minneapolis, ndipo ndidzakhala ku Heart's Harbor Tabernacle, ndi M'busa Gordon Peterson. Ndipo iwo ali ndi purogramu yowulutsa ndi kanema kumeneko. Chotero ngati muli—mukadzakhala chakumeneko, bwanji, zabwereni.

⁹ Ndiyeno pa twente-foro, kapena twente-faivi, kani, msonkhano waukulu udzayambika, ndipo ife tidzakhala kumeneko. Ndi purogramu yosazolowereka kwambiri. Bambo Roberts, Bambo Hicks, inemwini, azitumiki ena ambiri, adzakhala kumeneko. Ndipo palibe purogramu yomwe yaikidwa. A Christian Business Men, pokhala a Full Gospel Christian Business Men, iwo amafuna kuti angozisiya izo zotseguka, kwa chirichonse chimene Mzimu Woyera unganene kuti tichite; kudzakhala tonsefe kumeneko. Ndipo chotero iwo sanakhalepo ndi umodzi ngati umenewo, ndipo sanalengeze odzayankhula aliwonse. Kuyankhula kokha—kuyankhula kumene kukulengezedwa ndi—ndi m'mawa wa pa twente-firii. Ine ndikuyenera kuti ndidzayankhule pa kadzutsa wawo, ndipo izo zinalengezedwa. Kupanda kutero, ife tonse tidzakhala kumeneko, kumayembekezera pa Mzimu Woyera. Izo zikuyenera kukhala zabwino kwambiri, si choncho izo? Ngati ife titangodzipereka tonse kwa Mzimu Woyera, ndi zimenezotu, ndi kumulola Iye atigwiritse ife ntchito momwe Iye anga—Iye angafunire kutigwiritira ife ntchito. Tsopano . . .

¹⁰ Ndiyeno msonkhano wotsatira umene wakonzedwa, umene ine ndikuwudziwa, ndi Azusa Street Rally wakale. Ndi . . . Umenewo ukubwera pa Seputembala fifitini. Ine ndikatsegulira msonkhano kumeneko wa international rally for Azusa Street; zaka fifite za pentekoste mu United States. Iwo akwanitsa zaka fifite, Seputembala akubwerayu, pamene Mzimu Woyera unagwa koyamba mu Azusa Street Mission. Yakale . . . Ndikukhulupirira inali mishoni yakale ya Baptisti, kapena ku Azusa Street mu Los Angeles, California, ndi kumene Mzimu Woyera unagwa koyamba, zaka fifite zapitazo, Seputembala akubwerayu.

¹¹ Ndipo pamene ine ndinali ku Cow Palace, zaka zingapo zapitazo, ine ndinati . . . Chabwino, fifite, mawu oti *pentekoste* amatanthauza “fifite,” chotero bwanji osangokhala ndi msonkhano waukulu. Ndipo, inu mukudziwa, izo zinagwira

moto, ndipo akhala ndi msonkhano wapadziko lonse. Ndipo iwo udzakachitikira mu Angeles Temple. Ndipo masiku asanu izo zisanachitike, ndiyenera kukakhala ndi kuyang'ana kwa pozungulira ku malo osiyanasiyana. Oh, kumusi ku East Gate ndi...kapena ine ndikutanthauza South Gate, ndipo kumakwera mpaka ku—mzinda wa...Oh, ingapo ya mizinda yaing'ono imeneyo, mizinda isanu yosiyanasiyana, kuti ndikapange chithunzi pang'ono, msonkhano-wausiku umodzi, kenako nkudzapita ku—ku msonkhano waukulu.

¹² Ndipo ngati mudzakhale kozungulira California, kapena kunja uko, ena a inu ochokera ku California, mudzakumbukire zimenezo. Ife tikuyembekezera kudzakhala ndi nthawi yopambana ya chiyanjano ndi anthu a Mulungu panthawi imeneyo.

Tsopano tiyeni tipemphere.

¹³ Atate athu Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu, mmawa uno, chifukwa cha mwayi waukulu, waulemelo umene tiri nawo wobwera mu Kukhalapo Kwanu, ndi mitima yokondwera ndi kuthokoza, chifukwa chakuti Yesu Mwana wa Mulungu watilola ife kuti tichite izi. Ndipo chisomo Chake chatifikitsa ife mpaka nthawi ino. Ndipo ndife okondwa kukhala pano lero.

¹⁴ Wokondwa kukhala ndi malo ochepa awa osonkhanapo. Iwo ndi malo otseguka, Baibulo lotseguka, ndi mitima yotseguka kuti ilandire Mawu a Mulungu ndi Uthenga Wake. Ndipo ife tikupemphera kuti Mzimu Woyera ubwere ndipo udzadzaze mng'aru uliwonse wa mtima wathu ndi ubwino Wake, pamene ife tikuwereenga Mawu Ake. Pakuti kunalembedwa, “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Chotero, O Mulungu, tsegulani kamwa yathu lero, kuti mukhale Inu mukuyankhula, ndi mitima yathu, kuti ukhale Mzimu Woyera ukumvetsera. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, Mwana Wanu. Amen.

¹⁵ Lamlungu lapitali, mu Bukhu la Ahebri, tinayambira ndi mutu wa 10, ndipo kenako tinapita pa phunziro lina, osadziwa basi komwe Mzimu Woyera ungatizogolere ife kuti—kuti tiphunzitse kuchokerapo, panalibe chokonzekeeratu, timangoyembekezera pa kusuntha Kwake. Ife tinabwerera pa kudziwidwiratu, kuchokera pamenepo.

¹⁶ Kutu, tiri pomwepo, ndine wokondwa kumuwona Mlongo Hooper wakhala pamenepo, mmawa uno. Mlongo Flo, ndithudi wokondwa kukuwonani inu. Ambiri a inu mwina mukhoza kusamudziwa iye, ena a inu. Ndipo iye wakhala ali ndi chifuwa chachikulu kwa zaka ndi zaka, ndipo osachoka pa bedi, ndipo wayenda paliponse mu fukoli, kuyesera kuti apeze chiwombolo. Ndipo, lero, ndife okondwa kukhala naye iye mu kachisi, akuwoneka wabwino, lero. Mathokozo akhale kwa Mulungu!

17 Tsopano, wolemba Kalata ya Chihebri amaganiziridwa kuti anali Paulo, chifukwa zimamveka ngati zolembe zake. Ndipo Kalata ya Chihebri inali ya kwa Ayuda, Ahebri. Ndipo anali Paulo akuyesera kulekanitsa lamulo ndi chisomo, kuwonetsera—kusiyanana pakati pa chimene lamulo linali, ndi chimene chisomo chiriri, chifukwa Ahebri anali pansu pa lamulo. Ndiyeno Paulo anali kuyesetsa kuti awawonetse iwo chimene chisomo chinali. Ndipo ine ndikuganiza, inemwini, kuti mutu wa 10 apa, ndipo ndime ya 1, zikhoza kukhala poyambira pangwiro kwa chinthu chonsecho.

18 Tsopano ife tiri ndi mutu wa 1, poyambira. “Mulungu, mmasiku akale, mmachitidwe osiyanasiyana ankayankhula ndi makolo athu kudzera mwa aneneri, koma mu tsiku lotsiriza lino kudzera mwa Mwana Wake, Khristu Yesu.”

19 Kubwera pa mutu wa 7, kuwonekera kwa “Melkizedeki.”

20 Ife tinabwera mpaka pa mutu wa 9, wa “unsembe,” momwe Khristu akudzakhala Wamkulu Wansembe wathu, kuti adzatenge malo a wansembe wamkulu wakale.

21 Kenako tinazibweretsa izo pa mutu wa 10, ife tinabwera mu, “Lamulo kukhala mthunzi wa zinthu zimene zikubwera.”

22 Tinapita ku mutu wa 11, ndipo zonsezo ndi za—mithunzi yopambana ya chikhulupiro, ngwazi za chikhulupiro, momwe “mwa chikhulupiro” iwo anachita *zakuti ndi zakuti*. Ndipo momwe, “Popanda ife sakanapangidwa kukhala angwiro,” chifukwa iwo ndi a mthunzi wa ichi chirinkudza. Ndiyeno ife tinapita pa mutu wa 11, ndipo Paulo. . .

23 Kapena, mutu wa 12, Paulo akuti, “Powona kuti tazunguliridwa ndi khwimbi lalikulu chomwechi la mboni, tiyeni ife tiyike pambali cholemetsa chirichonse, ndi tchimo limene silimachedwa kutifooketsa ife, kuti tikathe kuthamanga ndi chipiro mpikisano umene wayikidwa patsogolo pathu.”

24 Mutu wa 13, mutu womalizira, anati, ukuthera apa, kuyandikira kumapeto, kuti Yesu Khristu ali zonse mu zonse, kuti, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Mukuona? Kusonyeza kuti anali Khristu mmbuyo lamulo lisanafike, anali Khristu mu lamulo, anali Khristu mmasiku a chisomo, ndipo adzakhala Khristu kwanthawizonse. “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawi zonse.” Ndi chithunzi chokongola bwanji chimene Kalata ya Chihebri ikutiambulira ife.

25 Tsopano, kuyambiranso tsopano ndi ndime ya 1, tiyeni tibwerere mmbuyo. Lamlungu lapitali, timaganiza kuti tifika pa mutu wa *Ungwiro*, komano Mulungu anatisunthira ife mmbuyo ndipo tinakapeza *kudziwidwiratu*, kutisonyeza ife kumene dziko lapansi lisanapangidwe nkomwe. . . Ndi angati anali pano Lamlungu lapitali? Tiyeni tiwone dzanja lanu.

Inu munazimvetsa izo? Dziko lisanapangidwe nkomwe, ife tinayikidwa mwa Khristu. Taganizani za zimenezo.

²⁶ Mulungu, pokhala wopanda malire, Yemwe sangathe kunama, sangayankhule chirichonse chosiyana, amadziwa chirichonse, wangwiro basi pachiyambi monga Iye aliri kumapeto, ndipo wangwiro basi pa mapeto monga Iye anali pachiyambi. Mulungu ndi wosatha, monga Umuyaya. Simungakhoze kupeza ngodya ya chozungulira changwiro. Inu mukhoza kuthamanga ndi kuthamanga kudutsa mibadwo, ndi Muyaya, ndipo sipangakhale konse, konse, sipadzakhala konse mapeto kwa izo. Ndipo umo ndi momwe Mulungu aliri. Ndipo pamene Iye akhala woyamba, anali. . . Mulungu, amene nthawizonse anali, Iye anali wopanda malire, wangwiro, kuyamba ndi kuyamba, ndipo nthawizonse Iye adzakhala chimodzimodzi. Iye sangasinthe konse. Iye ndi wangwiro chimodzimodzi.

²⁷ Tsopano unyolo wawukulu wangwiro uwu unadulidwa ndi danga la nthawi. Nthawi inadzabwera, chifukwa cha tchimo. Tiyeni tijambule chithunzi cha nthawi. Tiyeni tiwone mkombero wangwiro, kwanthawizonse, kwanthawizonse. Ndiyeno, zonse mwakamodzi, tchimo linadzagweramo, ndikudzayika—pang’ono. . . Monga mkazi wanga amazitchulira izo, “kachidindo” kakang’ono, kapena kabanga kakang’ono mu cholumikiziracho. Chotero, izo zinadzatsikira mmusi tsopano. Umuyaya ukupitirirabe, koma iwo siuli mu chikhalidwe changwiro. Pano pali danga laling’ono limene likutsikira mmusi, kudzaswekera mbali *iyi*, kukatulukira mbali *iyi*. Mulungu ankayenera kuchita zimenezo chifukwa ndi Satana anayambitsa zimenezo. Ndipo izo zinadzatsikira mmusi ku danga la nthawi, kuti akawayese, ndi kuwapanga angwiro, ndi kuwayeretsa iwo otaikawo. Kutu, Mulungu mwa chisomo Chake cha payekha, tsiku lina adzakhoze kudzakweza chidindo chaching’ono icho, kapena danga, kubwerera mu mkombero wangwiro, ndiye iwo ukupitirirabe chimodzimodzi basi. Inu mukuziwona izo?

²⁸ Nthawi! Tsopano, nthawi ndi kachingwe kakang’ono aka; iko kamalendewera pansu. Yesu anali wochokera ku Muyaya mpaka ku Muyaya, koma Iye anadzatsikira mu danga la nthawi ndipo anadzapangidwa kukhala thupi, ndipo anabwera kudzadutsa kuno kuti adzatiyeretse, kapena kudzaika chingwe cha Magazi paliponse kudutsa pa malo awa, kudzaliwombola ilo ndi kudzalilumikiza ilo ndi Mulungu kachiwiri, ku Muyaya wonse. Inu mukuziwona zimenezo? Ndicho chonse chimene nthawi ili.

²⁹ Kenako, Mulungu, pamene zinkayamba apa, kumapeto kwa kukhota kwakung’ono mu mkombero wangwiro, izo zinapanga izo kukhala zokhota pang’ono mmenemo. Pamene Mulungu anayamba pamenepo, Iye anali wangwiro. Chirichonse

chimene Iye ankanena chinali changwiwo. Chirichonse chimene Iye ankachita, amachita, ndi changwiwo.

³⁰ Chotero, ndiye, Baibulo linanena, kuti, “Khristu Yesu anali Mwanawankhosa wophedwa kuyambira,” chiyambi cha kukhota pang’ono, “chiyambi cha dziko lapansi.” Khristu anaphedwa pachiyambi. Tsopano, Iye sanaphedwe kwenikweni mpaka patadutsa zaka foro sauzande mtsogolo. Koma, chifukwa chimene Iye anaphedwera kumeneko, chifukwa, “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu.” Inu mukuziwona izo, M’bale Egan, chimene ine ndikutanthauza? Mukuona? Iye anali Mulungu, pachiyambi. Ndipo pamene. . .

³¹ Tsopano, Satana akhoza. . . sanatero—sanalenge kachingwe kakang’ono aka, ka banga kakang’ono aka. Iye sanalenge zimenezo. Satana sangathe kulenga. Satana amangokhoza kupotoza zimene Mulungu walenga.

³² Taonani, ine ndikunena izi kuti mumvetse. Iyi ndi kalasi ya akuluakulu, ndipo tonsefe ndi anthu okwatira, mwina nainte peresenti. Ndipo ndikuyembekeza kuti atsikana ndi anyamata akumvetsa liwu lawo, zomwe ine. . . Mundimvetse ine, ndikufuna ndifotokoze chinachake.

³³ Ngati mwamuna adzitengera kwa iyemwini mkazi, mzimayi, ndipo iye nkukhala mkazi wake, ndipo iwo nkumakhala limodzi ngati mwamuna ndi mkazi kwa zaka fifite; iwo amakhala oyera ndi angwiwo komanso osadetsedwa ngati kuti iwo sanadziwanepo wina ndi mzake. Izo, limenelo ndi dongosolo la Mulungu. Koma kuti mwamuna ameneyo kapena mkazi apite ndi kukakhala ndi mwamuna wina kapena mkazi, zimenezo zimapotoza, zimapangitsa ana apatchire kuti abadwe. Koma ngati iwo akhala limodzi mu mgwirizano wangwiwo umenewo, imeneyo ndi njira ya Mulungu. Koma Satana akabwerapo ndi kudzaika kusilira mwa mwamuna kapena mkazi, ndipo iwo nkumakhala motsutsana ndi malumbiriro a chikwati, ndipo kumeneko ndi kupotoza. Ndi chochitika chomwecho cha kugonana, koma chopotozedwa.

³⁴ Chotero icho ndi chimene Satana amachita ndi chinthu cholondola cha Mulungu, iye amapotoza icho. Ndi zimene Satana akuchita lero ndi chenichenicho, chapachiyambi (Mvetserani!), kwa Uthenga weniweni wa Mulungu: iye amawupotoza Iwo, amapanga china chakenso, amawupangitsa Iwo kumawoneka ngati chinachake chimene Iwo siuli.

³⁵ Mu dziko lero, ife tikupeza kuti alipo anthu, Baibulo linaneneratu izo, magulu atatu a anthu.

³⁶ Limodzi la iwo ndi wozizira, wokhuthala, wofunda, wosayanjanitsika, iwo amangopita chitsogolo, sichina kuposa kukhala wa ku loji. Iwo amapita ku tchalitchi, amakamba pang’ono za *ichi*, *icho*, ndi Ambuye, ndi zina zotero,

nkumabwerako, koma popanda chowachitikira chenicheni cha kubadwa mwatsopano. Oh, ena a iwo amadzinenera izo, koma moyo wawo umatsimikizira kuti sichoncho. Tsopano, zimenezo ziri kumbali inayo, kutali uko.

³⁷ Ndipo tsopano, kumusi kuno kumbali inayo, otengeka, ndi weniweni, mpingo woona, Yesu ananena chomwecho, “Akanadzakhala ofanana kwambiri, izo zikanadzakhoza kudzanyenga osankhidwa kumene.”

³⁸ Tsopano, anthu ambiri, mwamsanga akangowona kutengeka kutasakanizikana ndi chenicheni, “Ah,” iwo amati, “palibe kalikonse kwa Izo,” nkumapitirira. Mwaona, ndicho chinthu chomwecho chimene Afarisi anachita. Satana, samapusa akamayesera kupotoza izo. Iye akuyesetsa kuti apotoze Choonadi ichi. Ndipo wotengeka uyu apa akuyesetsa kuti atsanzire Choonadi chimenecho. Mukuona? Pamenepo ndi pamene pali mzere wanu wa ngozi, pomwe apo.

³⁹ Tsopano, izo zikutikakamiza ife kukhalabe auzimu, kumawerenga Mawu. Ndipo chirichonse chimene chiwuka, kunja, chotsutsana ndi Mawu, ndiye chitayireni icho kumbali. Ndi chifukwa chake, nthawi zambiri, kuti ine ndi . . .

⁴⁰ Iwo amati ndimakakisa kwambiri pa alaliki achikazi. Baibulo limanena kuti iwo asayankhule mu tchalitchi. Baibulo limawaletsa iwo kuyankhula mmalirime, kapena chirichonse, mu tchalitchi. Ine ndimayenera kukhala ndi Mawu, kuwawona pamene Iwo ali, kumawayang’ana Iwo.

⁴¹ Mu dziko lero, kumene timizimu tonseti tikuwukako, muwone, miyambo yonse yosadya nyama. Ndipo azamalamulo, amati, “ndiyenera kuchita *chakuti-ndi-chakuti*. Ngati sindiyankhula ndi malirime, ngati sindichita *ichi*, ngati sindifuula, ngati sindivina, pali chinachake cholakwika ndi ine.” Kumeneko ndi kutsatira malamulo.

⁴² “Ife tinapulumsidwa mwa chisomo, kudzera mchikhulupiriro.” Palibe chimene inu munachita; ndi zomwe Iye anachita. Iye anachita zomwe simukanakhoza kuchita. Ngati inu mukanakhoza kudzipulumutsa nokha, ndiye Iye sibwenzi atasowa kuti adzafe. Koma Iye anafa, ndi cholinga chakuti adzakupulumutseni inu, pamene inu simukanadzipulumutsa nokha.

⁴³ Mwambi wakale wosalemekeza Mulungu uja, umati, “Mulungu amathandiza iwo amene sangathe kudzithandiza okha. . .” Kapena, “Mulungu amawathandiza iwo amene amadzithandiza okha,” iwo amatero. Izo zangosinthanitsidwa. Ngati inu mungathe kudzithandiza nokha, Mulungu amayembekezera kuti muchita zimenezo. Mulungu amawathandiza iwo amene sangathe kudzithandiza okha. Ndipo inu simungadzithandize nokha, kuti mupulumutsidwe, chotero Mulungu, mwa chisomo Chake, anakupulumutsani inu.

44 Tsopano, zindikirani kukongola kwake. Lamulo, lalikulu mu Muyaya, momwe Mulungu anawoneratu izi. Ndipo ngati Iye alibe malire, ndipo sangathe—sangakhale china chirichonse. Ndiroleni ine ndingotenga izi, pafupifupi maminiti faivi, kuti ndilondolere izi pansi, mothinita, ndikhomerere izo, kuchitira kuti zisakupulumukeninso mmaganizo mwanu. Mulole Mzimu Woyera ubwere ndiye kudzawotcherera izo pamodzi ndi chikondi, kuti inu musadzazisiye konse izo.

45 Tsopano taonani. Mulungu, Amene sanganame; Mulungu, Amene ali wopanda malire. Ndipo ine ndikunena izi kenanso chifukwa cha anthu amene samawoneka kuti amakhazikika pa machiritso Auzimu. Ngati Mulungu analonjeza izo, Mulungu akuyenera kusamalira lonjezo Lake. Sangalisiye ilo.

46 Tsopano taonani. Iye asanawaike konse Mawu osindikizidwa, ndipo, *Awa* ndi malingaliro a Mulungu. Ndi Awa Apa. Awa ndi malingaliro a Mulungu, amene Iye anawaganizira, asanaikidwe konse maziko a dziko lapansi. Ndi zimenezotu. Ndi chifukwa chake Iye anayika Izo pa Mawu osindikizidwa, ndi kunena zomwe zikanati zidzakhale, chifukwa Iye anaziwona Izo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, ndipo anadziwa chimene Izo zikanadzakhala, ndipo anayankhula Izo.

47 Ndiyeno Iye anapereka chidziwitso Chake kwa aneneri, ndipo iwo anazilemba Izo. Ndipo chaka ndi chaka, ndipo zaka zana ndi zaka zana, ife taziwona Izo zikukwaniritsidwa chimodzimodzi basi. Mulungu, akupereka mithunzi ya Zakale, kuti zikawonetsere mthunzi wa Zatsopano. Ndipo ife tikuwaona Iwo, Mawu ndi Mawu, akukwaniritsidwa. Tikuyenera kuti takhazikitsa chikhulupiriro chotani mwa Mulungu!

48 Tsopano muwoneni Iye, “Khristu kuphedwa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe.”

49 Pamene Mulungu anayang’ana pansi ndi kuwona chinthu chokhacho chimene chikanapulumutsa munthu wotayika, Iye anati. . . Sindikudziwa ngati awa ali mawuwo, koma iwo amayenera kuti anali chinachake monga chonchi. “Munthu sangapulumsidwe, chifukwa iye akachimwa. Koma Ine ndikayang’ana pansi pamene ndipo Ine ndikuwona makumi amasauzande a mitima yowona imene ikufuna kubwera. Ine ndikuwona anthu masauzande amene akufuna kuti apulumutsidwe, ndipo sakufuna kuti adzapite mu chiwonongeko chowopsya ichi chimene Ine ndikuyenera kumupangira mdierekezi ndi angelo ake, chifukwa iwo akuyenera kudzalowa mu chilango chosatha. Ndipo anthu owona-mtima adzaziwona izo. Ndipo Ine—Ine ndidzakhala naye munthu wa dzina lake Esau; padzakhala wina, Yakobo. Ndipo Yakobo sadzakhala wabwino kwambiri, kuyamba ndi kuyamba, koma mu mtima mwake iye adzakonda zinthu za Mulungu, chotero Ine ndidzamusankha Yakobo.”

⁵⁰ Iye anakuwonani inu ndipo Iye anadziwa kuti mumafuna kupulumutsidwa. Chotero Iye anati, “Chinthu chokhacho chimene Ine ndingachite ndikupita pansi, Inemwini, ndikudzabadwitsa Mwana wamwamuna, kapena thupi lanyama, ndi kudzapangidwa mofanana ndi iwo.” Mankhwala ake ndi akuti Mulungu Mwiniwake adzakhale tchimo, kuti Iye adzakhoze kulipira mtengo. Chifukwa, zingatengere chinthu chapamwamba kwambiri chimene chiripo, kuti chimuchotse munthu ku chikhalidwe chotayika.

⁵¹ Ndipo, taonani, Iye ali pamwamba pa Mngelo aliyense, Mngelo wamkulu aliyense. Wapamwamba kwambiri amene analipo, anatsika pansi pano pa dziko lapansi, ndipo anadzakhala pakati pa munthu. Ndipo anapita kumzinda wotsikitsitsa kwambiri padziko lapansi, Yeriko. Ndipo anali wotsika kwambiri, mpaka munthu wamng’ono kwambiri mu mzindawo amachita kumuyang’anira pansi Iye; Zakeyu. Ndipo, ndiye, anafera machimo a munthu. Anabwera mwanjira ya khola, wosauka. Wolemera kwambiri. . . Oh, ndikuyembekezera kuti inu mukuzimvetisa izo. Wolemera kwambiri anadzakhala wosauka kwambiri.

⁵² Ngakhale pa usiku wamkuntho, anati, “Mbalame ziri nazo zisa, ndipo nkhandwe ziri ndi mphanga, koma Ine ndiribe ngakhale malo oti nkugonekapo mutu Wanga.” Wapamwamba wa mmiyamba monse mwa Kumwamba, anadzakhala wotsikitsitsa wa otsika onse. Ngakhale kwa moyo wa zinyama, zinali nawo mwayi, kwa Iye, kumuposa Iye, kunena za wofuwofu wa moyo.

⁵³ Osati zokhazo, koma, mu imfa Yake, Iye anavutika ndi imfa kumuposa amene anayamba wavutikapo; sizinachitikepo, mwa munthu, amene anavutikapo ndi mtima wosweka chotero mpaka Magazi Ake ndi madzi zinalekanitsidwa Iye asanamwalire.

⁵⁴ Wosaukitsitsa; kuchoka kukhala wolemera kwambiri, kudzakhala wosaukitsitsa. Kuchoka kukhala wodalitsika kwambiri, kudzakhala wovutika mowawa kwambiri. Ndiyeno, pambali pa zimenezo, anapita pansi kumalo otsikitsitsa kwambiri a gehena wotsikitsitsa, atanyamula tchimo lathu. Ndipo anakapeza pothera pa chingwe, kapena mapeto a chingwe, kuchokera pokhota. Pamenepo, anachinyamula icho mu chiukitsiro, ndipo anakachilumikizitsa icho ndi gawo lina la Muyaya, ndipo anapanga Msewuwawukulu wa chiyero, kuti osayera adzakhoze kubwera ndi kudzayeretsedwa:

Kudzera mu Kasupe wodzazidwa ndi Magazi,
Wochokera mmitsempha ya Emanuele,
Pamene ochimwa akagwera pansi pa
kusefukirako,
Ataya banga lawo lonse la kulakwa.

⁵⁵ Bwerani pa Msewuwawukulu. Ndipo tsiku lina, Iye Yemwe anali pachiyambi cha nthawi, adzaima ngati wamakedzana wa nthawi, ndipo adzakoka chingwe chachikulu cha Uthenga. Ndipo onse amene ali mu Msewuwaukuluwo, kuyambira kumayambiriro a nthawi, mpaka ku nthawi yamakedzana, mpaka kumathero a nthawi, adzakwezedwa mmwamba; pamene Iye azidzatenga nthawi kuchoka mu kukhalapo, kukalowa ku Muyaya. Inu mukuziwona izo? Ndi Uyo apo, “Wamphamvu weniweni yekhayo; Mfumu ya mafumu, ndi Ambuye wa ambuye.”

⁵⁶ Kodi Iye anachita izo motani? Kudziwidwiratu. Iye anadziwa. Atatero Iye ananena, kuti, “Iye anali Mwanawankhosa wophedwa.” Kenako, ngati Iye anali, zaka foro sauzande mtsogolo izo zinadzangobweramo, nthawi inatha. Iye anabadwa, iwo anachita kwa Iye zimene Iye anati iwo akanadzachita, ndipo kenako Iye anapachikidwa ndi kuphedwa. Koma, molondola, “Iye anaphedwa dziko lisanayambe,” pakuti Mulungu anamuwoneratu Iye ndipo ananena zimene zikanati zidzachitike. Ndipo pamene Mulungu ayankhula, zimayenera kutero. Inu mukumvetsa izo? Oh, mai! Mulungu anamuwoneratu Khristu, ndipo ziyenera kutero. Ndi chifukwa chake izo zinatha kale. Pamene Mulungu ananena Mawu, izo zinatsirizitsa izo. Chimenecho ndi chifukwa chimene Iye anawonetseredweratu, anaphedwa, pamene Mulungu anayankhula Mawu dziko lisanakhalepo.

⁵⁷ Zindikirani! Sikuti Khristu anangophedwa, kuti adzachotse tchimo, koma dzina lanu linalembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Mulungu analemba dzina lanu, analiyanjanitsa ndi Lake, maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe.

⁵⁸ Tsopano, Satana, amawapangitsa iwo kuti azichita mantha tsopano, amawapangitsa iwo kuti azikaikira izo?

⁵⁹ “Dziko lisanayambe konse, Mulungu anaitana dzina lanu, inu Akhristu, ndipo analilemba ilo mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa dziko lisanayambe nkomwe,” limatero Baibulo. Amenewo ndi Mawu a Mulungu, Iye anayankhula kumbuyo uko, ndipo anawulula kudzera mwa antchito Ake, aneneri, ndipo ife tikusangalala ndi mdalitso wa kupumula, ndi kudikirira pa Kudza kwa Ambuye. Kudikirira, mopirira. Izo zonse zatha. Oh!

⁶⁰ Nzosadabwitsa, matenda, zowopsya, imfa, palibe zimene zingatilekanitse ife ndi chikondi cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu! Chifukwa, maziko a dziko lapansi...Iye anatiyika ife pa Msewuwaukulu wakale umenewo, anakwera utawaleza wopingasa, anapita pa nsonga ya chiyambi cha nthawi kenanso, atagwira zingwe mdzanja Lake. Ndipo tsikulina, adzati, “Bwera kuno!” Ife amene tiri moyofe ndipo

tatsalira mpaka Kudza kwa Ambuye, sitidzawalepheretsa iwo amene anafa mu Msewuwaukulu, chifukwa lipenga la Mulungu lidzalira ndipo akufa mwa Khristu adzawuka. Ndipo ife tidzakwatulidwira mmwamba limodzi, kuti tikakumane nawo iwo, pamene chingwe chizidzakokeredwera mmwamba mu mkombero wa Muyaya. Ndiyeno pamene mibadwo ikupitirira, matamando Ake ife tizidzaimba.

⁶¹ Kodi Iye akuchita chiyani? Kumtunda kumeneko, akutimangira ife nyumba. “Mnyumba ya Atate Anga muli nyumba zambiri; ngati sizikanakhala chomwecho, Ine ndikanakuuzani inu. Ndipo Ine ndinabwera pansi pano, koma Ine ndikupita kukakukonzerani ena, ndikawakonza iwo onse. Ndipo ngati Ine ndikupita, Ine ndidzabweranso, kudzakulandirani inu kwa Inemwini.” Oh, mai! Ndipo Iye akukonza nyumba.

⁶² Pamene thupi lachivundi ili, limene liri kuno padziko lapansi, lidzakhala...ife tidzalekanitsidwa ndi ilo, ilo lidzaponyedwera kunja kwa chingwe cha Muyaya. Ilo lidzakhala kunja kwa phompho, limene palibe munthu angadzawoloke, kapena anawolokapo, kapena adzawolokapo. Ndipo pamene cholumikizira ichi pansi kuno, chidzakwera kufika ku gawo limenelo, ndiwo Msewuwaukulu wopalidwa, woyera, kumene Mulungu anati, pachiyambi, “kumene kunalibe kalikonse koyipitsa; palibepo chirichonse chowononga.” Ndipo tchimo linayambitsa kuzungulira uku. Ndiye pamene kuzungulira uku kukupitirizidwa, kumatsika mpaka kudutsa kuno kumabweretsa nthumwi, ndipo pamene iye adzakokedwa pamodzi, kuti akakumane ndi mathero aliwonse, Muyaya ukupitirirabe. Iwo amene ali owomboledwa azidzayenda mmenemo. Inu mukumvetsa zimenezo?

Oh, ine ndikukhumba ndikanaimba. Ine ndikufuna kuyimba nyimbo yakale ija:

Kuli nyumba yokongola kutali kutsidya kwa nyanja,
Kuli nyumba za chimwemwe za inu ndi ine,
Nsanja zonyezimira, dzuwa zidzaposi,
Nyumba yayikulu ya Kumwamba iyo tsiku lina idzakhala yanga.

Chotero, hema kapena kanyumba, ine ndizisamale chifukwa chiyani?
Iwo akundimangira ine nyumba yachifumu kumeneko!
Ya miyala yamtengo wapatali ndi madaimondi,
ndi siliva ndi golide,
Nkhokwe Zake ndi zodzaza, Iye ali ndi chuma chosaneneka.

Oh, chisomo chodabwitsa! kukoma kwakeko,
Chimene chinapulumsa wopandapake ngati
ine!

Ndinali wotayika, koma tsopano ndapezeka,
Ndinali wakhungu, koma tsopano ndikuwona.
(Palibe chimene ndinachita.)

Chinali chisomo chimene chinaphunzitsa
mtima wanga kuchita mantha,
Chinali chisomo chinachotsa mantha anga;
Chinawoneka mopambana bwanji chisomo
chimenecho

Ora limene ndinayamba kukhulupirira!

⁶³ Kudziwa kuti sichinali chirichonse chimene ndikanachita, kapena ndikanatha kuchita, kapena kuti ndinali ndi lingaliro, kapena kuti ndinali ndi mwayi woti ndingatero. Ndi zimene Iye anandichitira ine. Iye anatsika pansu ndipo anadzandiwombola ine, anadzandiika ine pa Msewuwaukulu; ndipo anadzaima kumapeto enawo, kuti adzakokere mbali zonsezo pamodzi, kuti adzapange Muyaya wopanda zingwe kuti uzipitirira. Ine ndiri nawo ufulu woyenda mu Muyaya umenewo chifukwa Iye anafa ndipo, mmalo mwanga, anandichotsera tchimo langa. Zodabwitsa!

*...lamulo pokhala nawo mthunzi—mthunzi wa
zinthu zabwino ziri nkudza...*

⁶⁴ Kodi mthunzi ndi chiyani? Mthunzi ndi chowonetsere cha chinthu. Inu mukudziwa, nthawi zambiri anthu amatenga Masalmo wa 23. “Eya, ngakhale ndingayende mu mthunzi wa mdima wa chigwa cha imfa.” Uko nkulakwitsa. Iyo inati iwo... Apo, “Eya, ngakhale ndingayende kudutsa mthunzi,” osati mthunzi wa mdima. Ngati ukanakhala mdima, iwo sibwenzi utapanga mthunzi. Pakuyenera kukhala gawo linalake la kuwala, kuti ziwonetsere mthunzi.

⁶⁵ Chotero, lamulo limapereka kuwala kokwanira kukawona mthunzi wa chinthu chenichenicho chimene chikubwera. Khristu anaimiriridwa mu lamulo limenero, la mthunzi.

⁶⁶ Iye anaimiriridwa, anawonedweratu, mwa Yosefe, pansu pa lamulo. Yosefe, pokhala mthunzi wa Khristu, wokonedwa ndi abambo ake, chifukwa iye anali mwamuna wauzimu. Iye ankawona masomphenya, ankatanthauzira maloto. Wauzimu kwambiri, ndipo wonyozedwa ndi abale ake. Mofanana, ndi Khristu. Iye ankawona masomphenya a abambo, ndipo iye anali mwamuna wauzimu. Ndipo m’bale wake ankamuda iye, popanda chifukwa. Ndipo iye anaganiziridwa kuti waphedwa, chovala chamagazi chitayikidwa pamaso pa abambowo.

⁶⁷ Oh, ndi zokongola bwanji! Oh, ndikayamba pa zimenezo, sindifika ku phunziro ili. Chovalacho, anapita nacho kwa bambo ake, chamagazi, kuimirira kuti mwana wake wafa; Isaki. Ndipo

lero, chovala cha Ambuye Yesu, moyo Wake woyeretsedwa ndi Magazi Ake okhetsedwera ochimwa, chiri pamaso pa Mulungu ngati chikumbutso kuti mtengo unalipiridwa. Inu mukuziwona zimenezo?

⁶⁸ Ndipo iye anagulitsidwa kwa pafupifupi zidutswa sarte za siliva, monga zinachitikira ndi Khristu. Iye anachotsedwa mdzenje, mnkhuti, mmene iye anaponyedwamo. Ndipo Khristu, nayenso, anategedwa kuchotsedwa mmanda. Ndipo anadzakhazikidwa ku dzanja lamanja la Farao. Panalibe munthu yemwe amakhoza kupita kwa Farao, kupatula kudzera mwa Yosefe. Kulengeza kumachitika, konena, pamene Yosefe akubwera, kuti iwo amapita, amuna patsogolo pake, oyitana, kumati, “Aliyense apinde bondo! Yosefe akubwera.”

⁶⁹ Tsopano, Baibulo linanena, kuti, “Bondo lirilonse lidzagwada, ndipo lirime lirilonse lidzavomereza, kwa Dzina la Ambuye Yesu.”

⁷⁰ Iye amakhoza kumumanga wantchito wa Farao mwakufuna kwake. Iye anali ndi mphamvu zonse ndi ulamuliro wa Igupto utaperekedwa mmanja mwake. Ndipo pamene galeta imagudubuzika mu msewu; aliyense, pamene kufuula kukubwera, wa chi Igupto aliyense, zinalibe kanthu kuti ankamuda moyipa bwanji iye, iwo ankagwadira bondo lawo kwa Yosefe.

⁷¹ Tsikulina, mzanga wochimwa, ziribe kanthu momwe iwe ungapunire kuchitcha Icho “kutengeka,” ziribe kanthu momwe mukufuna kunena kuti Izo nzolakwika, momwe mukufuna mutamazipindira ndi kumakhala mdziko, ndi kunyoza Mpingo ndi zinthu za Mulungu, tsiku lina inu mudzagwaditsa bondo lanu kaya mukufuna kutero kapena ayi.

⁷² Koma izo zingakhale zaulemelero bwanji kwa iwo amene amamukonda Yosefe. Momwe iwo ankamukondera iye, anati, “Oh, apa pakubwera kalonga wamkulu, Yosefe.” Ndipo iwo amagwaditsa bondo lawo, nkuti, “Oh, Yosefe, iwe wapulumutsa miyoyo yathu. Ife tikanafa ndi njala, ngati izo. . .”

⁷³ Koma, enawo, sanayamikire: “Ah, zamkutu!” Osathokoza. Tiri nawo anthu a mtundu umenewo mdziko lero. Inu simuzindikira kuti mkate kumene umene mumadya, komanso mpweya kumene umene mumapuma, umachokera kwa Mulungu. Ndipo iwo anamupembedza Iye.

⁷⁴ Kuno nthawi ina kale, pamene Bambo Baxter anali manenjala wanga. Pamene Mfumu yaku England. . . pamene ife tinali kumeneko kokacheza. Pamene mfumukazi inatulukira, dona wokonedwa, atavala mwinjiro wake wokongola, tsitsi lake la imvi. Ndipo mfumu itakhala, itadwala kwambiri pa nthawi imeneyo, iye samatha ngakhale kupirira zimenezo. Iye anali ndi vuto la mmimba komanso matenda ofoola ziwalo. Izo zinali iye asanapemphereredwe. Koma iye samatha ngakhale

kumirira. Koma, apobe, magazi achifumu a iye, iye anatulutsira chidali chaching’ono chimene iye anali nacho, panja, ndipo anayenda chotsika msewu ali mu ngolo.

⁷⁵ Bambo Baxter ataima pamenepo. Ndipo pamene iye amadutsa, ine ndinamuyang’ana iye. Milomo yake inali kunjenjemera, misozi imatsikira patsaya pake. Iye anadzayika nkono wake waukulu mondizungulira ine, anati, “M’bale Branham!”

Ine ndinati, “Inde, M’bale Baxter?”

Iye anati, “Inu mukudziwa, ndine—ndine waku Canada.”

“Inde.”

⁷⁶ Iye anati, “Mwamuna yemwe amalamulira dziko lathu, mfumu, iye ndi mkwatibwi wake wokonedwa ndi mkazake, akudutsa. Pamenepo ndi pamene ine ndikulephera kuti ndizigwire kumverera kwanga. Ine ndikuyenera kuwonetsera.”

⁷⁷ Ine ndinadzayika nkono wanga momukumbatira iye, ine ndinati, “M’bale Baxter, monga Mkhristu, ndi inu, zidzakhala bwanji tsiku lina la ulemelero, pamene Mfumu idzabwera ndi Mkwatibwi Wake!”

⁷⁸ Ngati munthu angaganize zimenezo pamene awona mfumu yapadziko lapansi, amene ndi wachivundi monga ife, zidzakhala bwanji pamene ife tidzawona Mfumu ya mafumu ikubwera mu Ulemelero? Idzakhala nthawi yaulemerero bwanji!

⁷⁹ Iye anawonetseredwa mwa Yosefe. Iye anawonetseredwa mwa Davide. Lamulo limawonetsa mthunzi wa Khristu. Davide...Khristu pokhala Mwana wa Davide. Ndiyeno pamene...Khristu pokhala mwa Davide, ngati mthunzi, zinamupangitsa Davide, pamene iye anachotsedwa pa mpando wachifumu, anakanidwa ndi abale ake omwe; osati abale ake okha, koma magazi ake omwe, Abisalomu, ndi ana ake omwe. Ndi izi apa. Iwo anawanyoza abambo awo omwe, ndipo ankafuna magazi ake, ndipo anamuchotsa iye pa mpando wachifumu. Ndipo Iye anakwera kupita ku phiri, phiri la Azitona, akuyang’ana mmbuyo, kumalirira pa Yerusalemu.

⁸⁰ Momwe kuti Iye, Mulungu, anawonetsera Khristu mwa Davide. Pakuti pamene Iye anadzachotsedwa pa mpando wachifumu, anakanidwa, ndipo nthumwi Zake zomwe, anthu Ake omwe, Ayuda, analirira Magazi Ake. “Sitikumufuna Munthu ameneyo!” Iye anadzakhala pamwamba pa phiri la Azitona ndipo amayang’ana pa Yerusalemu ndipo nkumalira, akuti, “Yerusalemu, O Yerusalemu, mmene Ine ndikanakusonkhanitsira iwe monga nkuku imachitira ndi anapiye ake, koma iwe sukufuna ayi.”

⁸¹ Khristu anawonetseredwanso mwa Melkizedeki, mu unsembe, pa mutu wa 9...mu mutu wa 7 wa Ahebri. Momwe Melkizedeki...Abrahamu nayenso anawonetseredwa, onse

kumbuyo uko, chinthu chabwino chonsecho, mthunzi chabe. Ndi momwe Melkizedeki, mu mutu wa 7, ife timawerenga za Iye apa. Ife tingowerenga Izo kwa kamphindi.

Pakuti Melkizedeki uyu, mfumu ya Salemu, wansembe wa Mulungu wammwambamwamba, amene anakumana ndi Abrahamu akubwerera kuchokera kokapha mafumu, ndipo anamudalitsa iye;

⁸² Ameni! Abrahamu! Loti, msuwani wake, anali atabwerera mmbuyo. Inu mukuwona Mzimu weniweni, woona wa Khristu? Ine ndikudalira kuti mukumvetsa zimenezo. Ziribe kanthu utali wa momwe iye anali atabwerera mmbuyo; pamene iye anali mu vuto, apa anadza Abrahamu kwa iye, ali ndi ankhondo. Alendo ozungulira kumeneko, kudutsa zigwa za Sodomu, anali atatsika ndipo anali atatenga Sodomu ndi mfumu yake. Ndipo anatenga, mmenemo, anamutenga Loti limodzi naye.

⁸³ Ndipo Abrahamu, amalume ake, m'bale mwamagazi, ana a mchimwene wake. Ndipo anayang'ana kumeneko ndipo anawona kuti mdani anali atamutenga wachibale wake wamagazi. Iye anapanga gulu la ankhondo la antchito ake omwe, anamutsatira iye.

⁸⁴ Zimenezo zinkaimira Khristu. Pamene Iye anawona kuti Mpingo wa Mulungu wamoyo unali utaitanidwako, mu kulakwa kwa mdierekezi, Iye anapanga gulu la Angelo ndipo anabwera padziko lapansi, kuti amutsatire mdierekezi, ndi kudzamugonjetsa iye. Aleluya! Kumubalalitsa mdaniyo! Oh, momwe ife tikumukondera Iye chifukwa cha izo! Anamugonjetsa mdaniyo. Ndipo Iye anamupha mdaniyo, ndipo anamulanda iye chirichonse chimene iye anali nacho; anamuponyera iye kumbali.

⁸⁵ Ndipo kodi chinthu choyamba chimene iwo anachita chinali chiyani, Abrahamu akubwerera ndi Loti, mkazi wake, ana ake, ndi zonse zimene iwo anali nazo, akuyenda mogonjetsa kubwerera ku malo awo akale kenanso? Iye anakakumana ndi Melkizedeki.

⁸⁶ Melkizedeki anali mfumu ya Salemu. Salemu ndi Yerusalemu. Pamene Ayuda anakalowa mu Yerusalemu, Iwo amawutcha iwo “Y- . . . -u-salemu,” Yerusalemu. *Salemu*, zimene zimatanthauza, “mzinda wa mtendere.” Iye anali mfumu ya . . . Mvetserani. Tiyeni tiwerenge izo.

Kwa iye . . . Abrahamu anapereka chakhumi cha zonse; poyamba pokhala . . . anamasulira Mfumu ya chirungamo, . . .

⁸⁷ Kodi Mfumu iyi imene inakumana naye inali ndani? Akubwerera ndi kupambana, ndi chigonjetso, monga Mpingo uliri lero, kuchokera ku Kalvare.

. . .pambuyo pake. . .Mfumu ya Salemu, amene ali, Mfumu ya mtendere;

Wopanda bambo, wopanda mayi, wopanda mtundu wochokerako, wopanda ngakhale chiyambi cha masiku, ngakhale kutha kwa moyo. . .;

⁸⁸ Kodi Mfumu ya ku Salemu inali ndani? “Mfumu yayikulu ya Yerusalemu,” osati wapadziko lapansi, Wakumwamba. Yerusalemu wa padziko lapansi ndi choyimira cha Kumwamba. “Ndipo apa pakubwera Mfumu ya Salemu, amene ali Mfumu yoyamba ya chilungamo, Mfumu ya mtendere; Iye analibe bambo aliyense, analibe mayi aliyense; Iye analibe chiyambi cha moyo, kapena mathero a masiku.” Oh, mai! “Wopanda mtundu wochokerako.” Palibenso wina koma Khristu Mwiniwake! Ndi Amene Mpingo ukukakumana naye pamene iwo udzakwera mu mlengalenga.

⁸⁹ Ndipo pamene Abrahamu anakumana naye Iye, iye anamupatsa Iye chakhumi cha zonse zimene iye anali nazo.

⁹⁰ Inu mukudziwa zimene iwo anachita? Chinthu choyamba chimene iwo anachita chinali kukhala pansi. Ine ndikumverera motengeka kwenikweni. Anadzakhala pansi ndipo ananyema mkate, ndipo anamwa vinyo, ndipo anadya mgonero, nkhondo itatha.

⁹¹ Ndipo Baibulo limatiuza ife, Yesu Khristu anatero, kuti ife tidzatero. . . “Sindidzadyanso za chipatso cha mpesa, kufikira Ine nditadzadya icho mwatsopano ndi inu mu Ufumu wa Atate Wangwa.”

⁹² Kuti, pamene nkhondo yomaliza idzamenyedwa, ndipo chigonjetso chapambanidwa, ndipo opatuka abwereranso ku Ufumu wa Mulungu, ife tidzakakhala pansu mu Ufumu wa Mulungu, ndi Melkizedeki wathu, Yemwe alibe chiyambi cha masiku, kapena mathero a zaka. Oh, mai! Iye ndi wopanda unyolo, Wamuyaya Uyo, tidzadya mgonero kachiwiri ndi Iye.

⁹³ Oh, ndi chithunzi chokongola bwanji chimene Chipangano Chakale ichi chikupereka kwa okhulupirira a Chipangano Chatsopano. “Lamulo pokhala nawo mthunzi wa zinthu zimene ziri nkudza, ndipo osati. . .” Mvetserani. “Lamulo pokhala nawo mthunzi wa zinthu zabwino zimene ziri nkudza, ndipo osati chithunzi kumene cha zinthu zimenezo.” Iwo unali mthunzi wa chithunzicho.

⁹⁴ Davide analamulira dziko lapansi, mu m’badwo wa golide wa Israeli. Kodi iye anali chiyani? Mthunzi. Davide atakhala pa mpando wachifumu, dziko lonse liri pa mapazi ake, kodi iwo unali mthunzi wa chiyani? Icho chinkapanga mthunzi wa Chinachake, kuphimba Mwana wa Davide, Amene ali Mwana wa Mulungu, Amene ali Melkizedeki, “amene chiyambi chake cha masiku ndi mathero a zaka, Iye alibe aliwonse.” Mthunzi wa,

nthawi ya Zakachikwi, Iye adzakhala pa Mpando wachifumu wa Davide ndi kumalamulira mafuko onse.

“Mthunzi wa zinthu zabwino.”

⁹⁵ Kodi izo ndi chiyani lero? Ife timayang’ana ndi kuwona mthunzi, amuna ndi akazi amene amadzinerana kuti ndi Akhristu, ndi kumakhala monga dziko lapansi. Iwo amati, “Oh, ndine wa tchalitchi. Zimapanga kusiyana kwanji?” Iwo ndi mthunzi wa wonyenga, kuchokera mmunda wa Edeni, amene ankanamizira kuti ndi wabwino, amene ankanamizira kuti anali ndi Kuwala, amene ankanamizira kuti anali ndi nzeru, koma anali wachinyengo. Ndipo umo ndi momwe amuna ndi akazi akuchitira lero, amene amatchula Dzina la Yesu Khristu ndipo samachoka ku tchimo, kuchitira mthunzi chilango chimene ati adzalandire ndi iye amene ali wachinyengo. Yesu ananena kwa Afarisi achipembedzo amenewo, “Inu ndinu a atate wanu mdierekezi.” Ine ndikudalira kuti muzipeza zimenezo. Ine ndikudalira kuti izi zikulowa mwakuya kwenikweni. Mthunzi wa chinyengo.

⁹⁶ Ndiye kodi amatani Mkhristu weniweni, wachifumu, wa handiredi peresenti amene wabadwa mwatsopano ndi Mzimu wa Mulungu, amene dzina lake linalembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe? Amene. . . Pabwere chiyani, papite chiyani, patani, iwo amagwiritsitsabe ku dzanja la Mulungu losasintha. Kodi muli chiyani mu mtima mwawo chimene chimachitira njala ya chinachake kumeneko? “Kwa iwo,” Baibulo linati, “amene amatero, amavomereza momveka bwino ndi umboni wawo, ndi moyo wawo, kuti iwo akufunafuna Mzinda umene uli nkudza, umene Wowumanga wake ndi Wowupanga ndi Mulungu.”

⁹⁷ Kodi njala imeneyo ndi chiyani mu mtima mwanu, mmawa uno, yofuna kuima mu Kukhalapo Kwake? Kodi njala imeneyo ndi chiyani mu mtima mwanu, m’mawa uno, kufikira ndi zonse zimene ziri mwa inu? Moyo wanu wonse ndi moyo wanu ukulirira chinachake, mpaka inu kumati, “Sindikusamala chimene chingabwere kapena kupita.”

⁹⁸ O Mulungu! Chinachake mwa inu, chikuyang’ana pa dziko lapansi, ndipo misonzi ikutsikira pansu mu mtima mwanu. “Oh, m’bale wotayika!” Kuwawona akazi mu njira zawo zonyozeka, zofowoketsa. Ndipo kuwawona amuna akumwa, ndi kumasuta, ndi kumatukwana, ndi kumatchova juga; ndi kumapita ku tchalitchi. Ndi chiyani mumtima mwanu chimene chimalira, “M’bale wanga wotayika, wobwerera mmbuyo”?

⁹⁹ Inu mwakhudza Chinachake *Apa*. Inu mwalumikizidwa ndi kumathero ena a chingwe. Inu mwakhudza a—chingwe, Msewuwaukulu, chimene chinamangiriza Muyaya pachiyambi. Pamene dzina lanu linayikidwa pamene, ndi kuwonedwa ndi chikhumbo chachikulu chimenecho, kapena kupsyinjika

kwa chidziwitso cha Mulungu, kunayang'ana pansi ndipo anawona kuti mudzabwera Kwanu. Ndipo, komabe, ochititsidwa khungu ndi zinthu za mdziko kuno, inu muli nalo lingaliro. Pamene Mzimu Woyera ukutsitsira pansi chingwe ichi cha magari, ndi kudzagwira mtima wanu, Izo zimayankhula za Dziko labwinoko, ndi Malo abwinoko, ndi Mzinda wabwinoko. Chomwechonso, inu mukhoza kunena kuti:

Dzikoli si kwathu, Ine ndikungopitirira
Chuma changa chayikidwa mmwamba kutali
kupitirira mlengalenga.

¹⁰⁰ Mulungu akuyankhula. Kaya ndi chiyani, kwatani, kudzenji; mtima wanu ndi wokhazikikabe. Ndi mthunzi, mthunzi uli patsogolo panu. Icho ndi chimene chimapangitsa mthunzi. “Lamulo pokhala nawo mthunzi” wa ubatizo wa Mzimu Woyera. “Lamulo pokhala nawo mthunzi.” Ndi chifukwa chake Iye ananena, mu Baibulo, inu mukuyenera kutenga ndi kufanizitsa Malemba ndi Malemba, ndi kuwapangitsa iwo kuti adutse. Ndipo ngati iwo abwera, nthabwala mmenemo, kumbukirani, inu mwachoka pamzere. Mukhale mu njira imeneyo, uwo—mzere wa Lemba umenewo.

¹⁰¹ Tsopano, “Lamulo pokhala nawo mthunzi, silingakhoze konse kumupanga wopembedzayo kukhala wangwiro, silingakhoze konse kumupanga wobwerayo kukhala wangwiro. Pakuti . . .” Mvetserani, ndime ya 2. Ife tiyesera izo, mphindi faivi zotsatirazi. Penyani.

Pakuti ndiye iwo sibwenzi atasiya kuti azikhala akupereka nsembe? . . .

¹⁰² Ngati magari a ng'ombe zamphongo ndi mbuzi ndi nkhosa ndi ng'ombe, ndipo ngati mkulu wansembe anali dongosolo lolondola, ndiye bwenzi dziko likumapitirirabe. Imfa bwenzi itasiya pansi pa zimenezo. Inu mukumvetsa izo? Mulole izo zilowerere kwa miniti yokha. Ngati Kayafa, wansembe wamkulu, akupereka nsembe ya moyo wa nyama, kukanamupangitsa munthuyo kukhala wangwiro ndi kumupatsa iye Moyo Wamuyaya, ndiye sipakanakhala chifukwa choti china chirichonse chichitike. Izo bwenzi zikupitirirabe. Moyo Wamuyaya ukanabweramo, ndi kumakulabe chitsogolo. Koma pankayenera kukhala mthunzi wa Mwanawankhosa wa Mulungu weniweni amene ankabwera kudzachotsa tchimo la dziko lapansi, zimene zinayankhulidwiratu ndi Mulungu.

¹⁰³ Ndipo amuna ndi akazi lero, amene anadziwidwiratu ndi Mulungu maziko a dziko asanakhazikitsidwe, maina awo analembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Ngati iwo afuula, ziri bwino. Ngati iwo satero, ziri bwino. Ngati iwo achita *ichi*, ziri bwino. Ngati iwo satero, ziri bwino. Pakuti, Mulungu ananena kale chomwecho. Izo zikuyenera kudzachitika. “Si iye amene afuna, kapena iye amene

athamanga, ndi Mulungu amene amawonetsera chifundo.” Kusankha kwa Mulungu, osati kwathu.

¹⁰⁴ Tsopano zindikirani. “Ndiye nsembe zimenezo sibwenzi zitaleka kukhalapo? Pakuti izo sibwenzi zitasiya kumaperekedwa nsembe? chifukwa...” Bwanji? Apa ife tikufika kumapeto tsopano; sukulu yatuluka. “Chifukwa chakuti wopembedzayo...” Bwanji? “Chifukwa...” Oh, ine ndikumverera ngati mwana wamng’ono ali ndi chidole cha Khrisimasi tsopano. Ndine wokondwa kwambiri za Izi. Momwe ine ndimakondera kuzipereka Izo kwa Mpingo, kwa inu okhulupirira, kuti muwone chimene chiri Choonadi! Ngati izo zikanakhala zolondola, izo sibwenzi zitasiya konse; izo zikanamapitirirabe, Moyo Wamuyaya. “Chifukwa wopembedzayo...” Tsopano muwerenge Izo ndi ine, “Wopembedzayo kamodzi...” Osati chitsitsimutso chirichonse, mpaka Lamlungu lirilonse mmawa.

...koma wopembedzayo *akatsukidwa kamodzi*
ayenera kukhala...samakhalanso ndi chikumbumtima
cha tchimo.

¹⁰⁵ Chiyani? “Wopembedzayo akatsukidwa kamodzi.” Kuyeretsedwa ndi Mwazi a Mwanawankhosa, ukasesa kwathunthu kamodzi, umamutsuka wopembedzayo, chikumbumtima kumene cha tchimo chimachokapo. Taganizani za zimenezo.

¹⁰⁶ Mawu akuti *chikumbumtima*, mu kutanthauzira kolondola kumene ife tingakugwiritse ntchito apa. Ili ndi la mtundu wa King James. Mu England, zimatanthauza chikumbumtima. Apa, zingatanthauze “chikhumbo.” “Wopembedzayo akatsukidwa kamodzi,” ndi kuyeretsedwa ndi Khristu pa Kalvare, “samakhalanso ndi chikhumbo cha tchimo. Zinthu zakale zapita; zinthu zonse zсандulika zatsopano.”

¹⁰⁷ Tsopano, inu mukhoza kuyimba ngati timba, ndipo nkumakhalabe ndi udani, njiru ndi ndewu mu thupi lanu, mmoyo mwanu. Inu mukhoza kufuula ngati sindikudziwa chiyani, inu nkukhala nazobe izo. Inu mukhoza kuvina mu Mzimu, mukhoza kuyankhula ndi malirime, mukhoza kunenera, mukhoza kulalikira, chirichonse cha zinthu zimenezo, ndipo nkukhalabe ndi njiru, kaduka, ndewu mu mtima mwanu.

¹⁰⁸ Koma pamene kudzozedweratu kwenikweni, kowona kwa Mawu Amuyaya a Mulungu, pamene dzina lanu linkalembedwa mmenemo, ndipo Magazi nkumutsuka munthu ameneyo; malingaliro kumene a izo, amamudzudzula iye panjirapo pamene iye wayimapo.

¹⁰⁹ Anati, “Sizimanditsutsa ine. Ine ndimapita ku malo amenewa; ine sindimatsutsika.” Chifukwa chiyani sizitero? Inu, ngati wopembedza wa mthunzi, simunatsukidwe konse ndi Magazi a Yesu Khristu.

¹¹⁰ Ndipo azamalamulo anagwira lingaliro ili, “Aleluya, ndidzivala madiresi anga otsika pansi mpaka *chonchi*, ndi madiresi anga otsika pansi mpaka *chonchi*. Ine ndizilisiya tsitsi langa kuti litalike, ndipo ndizikhala bwino bwino.” Limenelo ndi bodza. Ndipo iwo amamuloza mkazi amene ali ndi tsitsi lalifupi, ndi wa madiresi aafupi, ndikuti, “Iye akupita ku gehena.” Ine sindinganene zimenezo. Koma ndikuganiza kuti zinthu zimenezo ndi zabwino bwino. Ine sindikuwadzudzula iwo. Koma pamene inu mukhazikitsa ziyembekezo zanu za Muyaya ndi chipulumutso pa chiphunzitso chimenecho, inu mwathedwa limodzi ndi izo.

¹¹¹ Mwamuna kapena mkazi, ziribe kanthu kuti ndinu *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*, inu mubwere ku kasupe wodzazidwa ndi Magazi ochokera mmitsempha ya Emmanuele, ndipo mulole kuyeretsa kwa Magazi a Ambuye Yesu Khristu kuyeretse machimo anu.

¹¹² M'bale, izo sizingakhale kanthu, mukhoza kukhala ndi madiresi otalika kwambiri, inu mukhoza osavala malaya a mikono yaifupi, amuna inu, ndi zinthu zimenezo, kapena chirichonse chimene inu mukufuna kuchita; koma ngati mukadali ndi dumbo, ndi njiru ndi udani. Inu mwinamwake munathamangapo, munavina, munayankhula mmalirime, munafuula, munalalikira Uthenga, kapena chirichonse, koma inu mwatayika mpaka Magazi amenewo atakutsukani ndi kudzakhazikitsamo chikondi Chaumulungu cha Ambuye Yesu Khristu, mu mtima mwanu, ndi kusiya zidindo za Moyo wa Khristu mmbuyo mwanu. Amen.

¹¹³ “Pamene pali malirime, iwo adzasiya. Pamene pali uneneri, iwo udzalephera. Pamene pali chidziwitso, icho chidzatha. Koma pamene icho chimene chiri changwiwo chidzabwera, icho chimene chiri cha mderamdera chidzathetsedwa.”

¹¹⁴ Ndipo ife tikupumula lero, monga a malamulo, pa chinthu china chalamulo chimene tinachita. Bwanji, pamene ine ndinali wochimwa, ine ndinali kambuku. Mochuluka momwe ndinkayesera kusiya *ichi* ndi kusiya *icho*, ndinkangopangitsa kuti mangamanga anga kuti aziwala kwambiri. Ine ndinali wachinyengo ndi izo, ndipo chomwechonso inu. Koma tsiku limene inu munadzabwera ku Kalvare, kuti mudzayeretsedwe, kumene Mwanawankhosa weniweni. . .

¹¹⁵ Pansi pa Chipangano Chakale, iwo ankamubweretsa mwanawankhosa. Iwo ankapita kunja ndi kukachita chigololo. Iwo amakhoza kupenga, ndi kumakangana, ndi kumamenyana, ndi kumatukwana. Ndipo, pamene iwo atero, iwo ankamubweretsa mwanawankhosa, ankapita naye kwa wansembe, ndikukati, “Oh, wansembe wa Mulungu!”

“Inde?”

116 “Ine ndinamtukwana woyandikana naye wanga. Ine—ine ndinachita chigololo. Ine ndinanena bodza. Ine ndinaba.” Amaika manja ake pa mwanawankhosa wakufa uyu, wopanda banga. Wansembeyo ankamufufuza iye; amayenera kusungidwa, kuti awone ngati anali wolondola. Amayika manja ake pa iye, ndipo iwo ankadula pakhosi. Ndipo magari anakwera pamwamba pa manja ake, ndipo mwanawankhosa wamng’ono akuphiriphitha, akukankha, ndi kumafa.

117 Ndipo wopembedza atayima pamenepo, ankati, “Inde, ameneyo amayenera kukhala ine, koma mwanawankhosa akutenga malo anga.” Koma iye anakabwererako ali ndi chikhumbo chomwecho. Iye anakachitanso izo kenanso mwamsanga akangopeza mpata.

118 Ndipo umo ndi momwe anthu amachitira lero. Iwo amabwera ndi kudzavomereza, ndikuti, “Ine ndachita *ichi, icho*, kapena *chinacho*,” ndipo nkubwerera kumeneko; ndi kukatembenukanso, nkumakachita chinthu chomwecho kenanso. Kujowina mpingo umodzi, wina; ngati uyu ayambitsa kenakake kakang’ono, chabwino, kupita kwa *uyu* ndi *uyu*.

119 Koma izo zinali mthunzi wa chiyani? Izo sizinali zangwiwo. Izo sizikanakhoza kuchotsapo tchimo, koma izo zinali mthunzi wa kuchiritsidwa kwenikweni kwa pawiri kukubwera.

120 Ndipo pamene Yesu Khristu Mwana wa Mulungu anabwera, ndipo nkudzafa pa Kalvare, ndipo wopembedzayo akayika kamodzi manja ake pamutu pa Ambuye Yesu, ndipo nkudziwa kuti kukuwa ndi kulira pamtanda, imfa imeneyo, kuzunzika kowopsya kumeneko, iye amayenera kuti azilipire iyemwini, mu kuya kwa gehena uko kumene iye akanati apiteko. Iye ankadziwa kuti Khristu analipira malo oti avomereze tchimo lake.

121 Ndiye chimachitika ndi chiyani? Nchiyani chimapangitsa kusiyanako? Nchiyani chimatuluka mwa mwanawankhosa, kuchokera mmagazi? Umapita moyo. Ndipo khungu la magari linali mdzanja lake. Moyowo unali ukuzungulira paguwa, koma moyo wa mwanawankhosa sukanabwerera pa wopembedzayo; ngakhale iye atavomereza kuti iye walakwitsa, ndipo mwanawankhosa anatenga malo ake. Chifukwa, wopembedzayo ali ndi solo, ndipo sakanakhoza kukhala ngati nyama. Kulondola.

122 Koma, O Mulungu, mukhetthemulenso nyundo zonse ziwiri pa mfuti, ndipo mulole mipope iwiri yonse ipite ku tchalitchi ichi, ndiro pemphero langa. Koma pamene wopembedza . . .

123 “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha, Mzimu Woyera. Sadzabwera ku chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.”

¹²⁴ Pamene wopembedzayo ayika manja ake pamutu wa Mwanawankhosa wakufa wa Kalvare, ndipo nkuvomereza machimo ake, ndipo Mulungu nkuzindikira kuti zimenezo nzoona zochokera mumtima mwake. Iye wavomereza tchimo lake. Moyo wozungulira uja, wotchedwa Mzimu Woyera wa Yesu Khristu, umapotolokeranso kwa wopembedza. Ndipo iye amatsukidwa, ndipo samakhalanso ndi chikhumbo cha tchimo. Pakuti iye akutsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, ndipo osati moyo wake womwe, kuyambira pamenepo mpakana. Iye azilakwitsa, ndithudi, koma Moyo umenewo uzimugwirabe iye.

¹²⁵ Penyani. Tiyeni tipite mmusi ku foro- . . . Ndime ya 14. Ife tiribe nthawi kuti timalizitse izi. Tiyeni titenge ndime ya 12.

*Koma munthu uyu, (osati mwanawankhosa) . . .
Khristu!*

Koma munthu uyu . . .

¹²⁶ Iye akuyankhula tsopano za dongosolo la mkulu wansembe. Momwe wansembe ankalowera mkachisi, ndi zina zotero; kukapembedza. Momwe wopembedzayo ankabwererako ndi chikhumbo chomwecho. Munthu amabwera paguwa ndikuti, “Inde, sindikufuna kupita ku gehena.” Mlaliki akalalikira za momwe gehena aliri wotentha, ndipo guwa limadzaza ndi anthu. “O Mulungu, sindikufuna kuti ndidzapite ku gehena.” Koma iwo samakhala ololera nkomwe kuti adzipereke okha, ndikuti, “Inde, Ambuye. Osati kufuna kwanga, kuyambira tsopano mpakana, koma Kwanu.”

¹²⁷ Kuzindikira kwenikweni chimene mukuchita. Ndikuti, “Mulungu, ndichitireni ine chifundo.” Magazi a Yesu ali mmanja mwanu ndiye. Musapite kunja ndi kukayamba kukhala moyo womwewo umene munkachita. Magazi amenewo adzakutsutsani inu kumapeto, pa Chiweruzo. Inu kulibwino muzikhala nawo Moyo umene uli m’Magazi amenewo, kuti abwerere ku magazi a moyo wanu, abwerere ku mtima wanu ndi kudzakupangitsani inu kukhala moyo wosiyana Mkhri- . . . munthu wosiyana. “Wopembedzayo akatsukidwa kamodzi.” Penyani apa.

Koma munthu uyu, atatha kupereka nsembe imodzi chifukwa cha tchimo kwa (nthawi yayitali bwanji?) nthawizonse, (Umuyaya wopanda mapeto umenewo) . . . kwa nthawizonse, anadzakhala pansu ku dzanja lamanja la Mulungu; (Kumapeto a msewu.)

¹²⁸ Kodi Iye ali kuti? Kumapeto a msewu. Inu mukukumbukira, Lamlungu lapambuyo pa lapitali, Lamlungu limene ndinalalikira ndi kuwonetsera kachombo kakang’ono ka Mose, kamene kankapita kumusi kudutsa mmantcheza ndi chirichonse? Inu mukukumbukira momwe inu anthu okalamba munkalirira ndi kufuula, pamene ine ndinali kulalikira kwa ana? Ndinali nawo onse aja a maso aang’ono akuda ndi a buluu, atakhala apa pa mzere wapatsogolo, ndikuwauza iwo,

“Ngati mutaya moyo wanu, mudzaupeza. Ngati muwusunga moyo wanu, mudzautaya iwo.” Inu mukukumbukira zimenezo, mpingo?

¹²⁹ Inu mukukumbukira, pamene ine ndinali kuwonetsera, ndinkapereka kuwonetsera kwa mmawa kuja pamene Yokebedi ndi pamene Amramu, Aaroni ndi Miriamu, onse kumeneko asanafike masana, ndi manja awo ali mmwamba, akuti, “Mulungu, Inu munatipatsa ife mwana, tsopano tikumubwezera iye kwa Inu. Inu munampereka iye kwa ife. Iye sanali wathu; iye anali Wanu. Inu munampereka iye kwa ife, ndipo tsopano ife tikumubwezeretsanso iye kwa Inu.” [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. “Ife tikamusunga iye, mfiti za gehena zidzamupha iye. Akazi achikulire a mphuno zazitali awo azibwera kuno ndi kudzatenga mutu wake wawung’ono ndi kudzawumenyetsa iwo pa khoma. Ife timutaya iye ngati timusunga iye. Koma ngati ife timubwezera iye kwa Yemwe anampereka iye kwa ife, ife timusunga iye.”

¹³⁰ Ndicho chinthu chomwe chomwecho mu khungwa lanu laling’ono, mmawa uno, m’bale, mlongo. Inu muli ndi katundu mmenemo, katundu wofunika kwambiri yemwe anayamba wakhalapo. Iye amatchedwa solo yanu. Kazipitani patsogolo, isungeni iyo, khalani momwe mukufunira, mudzaitaya iyo motsimikiza basi monga ndikuimira pano. Ndipo ngati muyipereka iyo kwa Mulungu, ndi kupereka chifuniro chanu, mudzayisunga iyo. Mudzaipeza iyo. Yesu ananena chomwecho. Kumbukirani.

¹³¹ Ndipo pamene iwo anakankhira izi, chuma cha mtima wawo, pamene iwo anakankhira kunja mu mtsinje, ng’ona zakale zikubwera. Ine ndikukhoza kumuwona Mulungu, monga ine ndinanena, akukwera kuchokera pa Mpandowachifumu Wake.

¹³² Inu mukudziwa, pali mayesero ambiri amene amachitika kumusi kuno. Koma pali Winawake amayang’ana pa iwo, nthawi zonse. “Iwo sanakonde moyo wawo kufikira imfa.”

¹³³ Pamene Amramu wokalamba wosauka, ndi mwana wake yekhayo, wokonedwa wamng’ono. Yokebedi wamng’ono anali atangomuyamwitsa kumene iye pachifuwa chake, ndipo kenako amayenera kukamuyika iye mu kachombo ndi kukakakankhira iko mu mantcheza, kumene ng’ona zinanenepa chifukwa chodya makanda aang’ono. Pamenepo, pamene iye anali ataima pamenepo, ndipo misozi ikutsikira mmasaya mwake, Mulungu anati, “Bwera kuno. Gabriele, bwera kuno miniti. Ine ndikufuna ndikuwonetse iwe chinachake. Ine ndiri ndi winawake amene amandikhulupirira Ine kwenikweni.” Amen.

¹³⁴ Mulungu, ndiroleni ine ndikhale munthu wa mtundu umenewo, amene angati, “Mulungu anatero. Izo nzowona.” Ndi kukhala wakufa kwambiri kwa china chirichonse, mpaka icho nkukhala mkuwa wophokosera kapena nguli yozungulira.

¹³⁵ Anati, “Bwera kuno, Gabriele. Angelo nonse inu tulukani kuno. Ine ndikufuna ndikuwonetseni inu chinachake. Mukumuwona mwamuna uyo kumusi uko wakweza manja ake mmwamba? Iye anamukankhira mwana wake yemwe. Ine ndinampereka iye kwa iye, tsopano iye akumubwezanso iye. Ine ndiwonetsetsa kuti iye amusunge iye.” Ameni. Anati, “Gabriele, itana Angelo teni sauzande, ayambe kuguba. Ine ndikuwafuna iwo kunjā kuno.”

¹³⁶ Gabriele analiza lipenga laling’ono, ndipo ilo linadutsa makonde a Muyaya. Angelo teni sauzande okhala ndi zida anayamba kuyenda.

¹³⁷ Anati, “Muzimangirize nokha chokwera ndi chotsika mtsinjewu. Muwonetsetse kuti pasakhale ng’ona, china chirichonse, chimene chingakhudze mmodzi wa iwo. Iye waperekedwanso kwa Ine.”

¹³⁸ Gabriele anati, “Ambuye, Kalonga Wamkulu, Inu mukakhala kuti?”

¹³⁹ “Ine ndikakhala kumapeto kwa mzere. Ine ndizikalandira kumusi uko.”

¹⁴⁰ Ndicho chinthu chomwecho Iye akuchita lero. Pamene munthu ayika chidaliro chake mwa Ambuye Yesu, nkuvomereza tchimo lake, Mzimu Woyera umamugwira munthu ameneyo, ndipo Khristu amayima mbali yolandirira. Kudutsa mmadziwe ambiri, ndi ng’ona, ndi zipukupuku zowopsya, ndi zina zonse zimene tadutsamo.

Kudutsa mu zowopsya zambiri, zovuta, ndi
misampha,
Ine ndabwera kale;
Ndi chisomo chimene chandifikitsa ine
wotetezeka mpaka pano,
Ndi chisomo chimene chidzanditengere ine
Kwathu.

¹⁴¹ Nndani ali kumapeto kolandirira? Mvetserani:

...kwa nthawizonse, anadzakhala pansu ku dzanja
lamanja la Mulungu;

Kuyambira tsopano (kumtunda uko kumapeto kwa
msewu) akuyembekezera mpaka adani ake apangidwe
kukhala chopondapo mapazi ake.

¹⁴² Kodi mwakonzeka? Ndi izi apa. Ino ndi nthawi yomaliza pa boti. Awa ndi malo omaliza okhala ndi tochi. Apa pali kukhoma komaliza kwa msomali. Uyu ndi Mmodzi amene amagwira Muyaya mpaka Muyaya. Ndipo, mmenemo, Lupanga la chipulumutso cha Mulungu ladutsa kudutsa mu mtima, popachika nthumwi Zake, kwa Mzimu Woyera. Ndi izi apa, Ahebrī 10:14. Mvetserani. Osati mawu anga; koma Mawu a

Mulungu, Amene anawayankhula Iwo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Izo zikuyenera kukhala chomwecho.

Pakuti ndi nsembe imodzi iye wa (w-a-t-i-p-a-n-g-a-a-n-g-w-i-r-o) watipanga angwiro kwa nthawizonse amene ayeretsedwa.

¹⁴³ Watipangitsa angwiro mpaka liti? Kufikira nthawi yotsatira imene inu mudzakangane ndi woyandikana naye wanu? Kufikira nthawi imene mudzamuwone winawake, bambo wina kapena mkazi amene ali wosilira? Kufikira nthawi yotsatira imene mudzawona mwayi wonena bodza lalikulu? Kufikira nthawi yotsatira imene mudzawone pamene mungamugwire wina ndi kuwapweteka iwo, ndi kudzawathamangitsa ku tchalitchi, kotero nthawi ina mukhoza kumutsutsa winawake?

¹⁴⁴ “Iye watiyeretsa kwanthawizonse, watipanga angwiro kwanthawizonse. Kumene Mzimu Woyera...” Inu mukhoza kunena chinachake, nthawiyina, cholakwika. Uko nkulondola. Inu mukhoza kuchita chinachake, nthawiyina, cholakwika. Uko nkulondola. Koma mwamsanga inu mukachita zimenezo... Penyani ndime yotsatira.

Chimene Mzimu Woyera...

¹⁴⁵ Oh, mai, ine sindingakhoze kulalikiranso mopitirira. Penyani.

... Mzimu Woyera... ndi mboni kwa ife: ... (Mai!)

... Mzimu Woyera... ndi mboni kwa ife: ... zitatha izo iye anali atanena kale,

Ili ndi pangano limene ine ndidzapangana nawo mu masiku amenewo, atero Ambuye, Ine ndidzaika lamulo langa mumtima mwawo, ndipo mmaganizo awo Ine ndidzawalemba iwo;

Ndipo machimo awo ndi kusaeruzika kwawo sindidzakumbukiranso konse motsutsana nawo.

¹⁴⁶ O Mulungu! “Munthu aliyense amene ali ndi chiyembekezo ichi amadziyeretsa yekha monga Mulungu ali woyera.”

Tiyeni ife tipemphere.

¹⁴⁷ Atate Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu, mmawa uno, chifukwa cha kuyeretsa kwa Mzimu Woyera, chifukwa cha chisomo cha Mulungu wamoyo. Ife tinali ochimwa, osalungama, opanda umulungu, osakondedwa; opanda Mulungu, opanda chiyembekezo, osayanjanitsika mdziko, ndipo Khristu anabwera ndipo anadzatenga malo athu. Mwa kudziwidwiratu Mulungu anatiwona ife tiri mu chikhalidwe ichi, podziwa kuti tinali anjala ndi ludzu. Nzosadabwitsa kuti Yesu anati, “Iwo adzazadzidwa.” Osati “adzakhala membala.” Osati “iwo adzajowina.” Koma, “Adzazadzidwa; kuchita njala ndi ludzu la chilungamo.” Mwa kuyankhula kwina, “kuchita njala ndi

ludzu,” podziwa kuti sitingachite chirichonse mwa ife tokha, ziribe kanthu chimene tingachite.

¹⁴⁸ Mdierekezi akhoza kutipangitsa ife kutsanzira mphatso iliyonse. Akhoza kutipangitsa ife kupita kunja ndi kukayika manja pa odwala, ndipo iwo nkuchira. Akhoza kutipangitsa ife kuyankhula ndi malirime. Akhoza kutipangitsa ife kutanthauzira malirime. Akhoza kutipangitsa ife kukhala ndi nzeru, chidziwitso. Koma izo sizitengera izo, Ambuye.

¹⁴⁹ Inu munati, “Ambiri adzabwera tsiku limenelo, ndikuti, ‘Ambuye, Ambuye, kodi ine sindinachite zinthu izi mu Dzina Lanu?’” Iye anati, “Chokani kwa Ine, inu akuchita kusaeruzika. Ine sindinakudziweni inu nkomwe.”

¹⁵⁰ O Mulungu, ndiye mulole ziyembekezo zathu zisamangidwe pa china kuposa Magazi a Yesu ndi chirungamo.

Pamene zonse kuzungulira solo yathu zitha,
Ndiye Iye ndi chiyembekezo chathu chonse ndi
kukhalapo.

Pakuti pa Khristu, Thanthwe lolimba, ine
ndaima;

Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira.

¹⁵¹ “Kumudziwa Iye ndi Moyo,” osati kudziwa malamulo, “kumudziwa Iye,” Munthuyo.

¹⁵² Ine ndikumupempherera, Atate, wochimwa aliyense mchipinda chino lero, kuti Inu muwapulumutse iwo pakali pano. Ndipo mulole iwo, popanda kutengeka kulikonse, popanda zotsutsana zirizonse zochokera kwa mdierekezi; koma mulole iwo, ndi chikhulupiriro chowona, chosakanizidwa, akhulupirire chimene amva chikulalikidwa, ndipo awuvomereze Mzimu Woyera Umene unabweretsa Iwo. Perekani izi, Ambuye, pakuti ndi mu Dzina Lake ife tikupempha izi.

Ndipo ndi mitu yathu yoweramitsidwa.

¹⁵³ Ine ndikudabwa ngati pali winawake pano mmawa uno. . . Tsopano ndikufuna zanu. . . usinkhu, woota mtima, woota; ziribe kanthu zimene mwachita, ziribe kanthu kuti mwayamba kangati, kapena mwakhala nthawi yayitali bwanji mu tchalitchi. Kodi ndinu woota mtima, kuchokera pansu pa mtima wanu, za izi, amene mukudziwa kuti zinthu za mdziko zapita zachoka kwa inu? Kudziwa kuti, tsiku ndi tsiku, ndi chaka ndi chaka, izo zikupitirira, nangula wanu wagwira? Pali Winawake, kutsidya, anaphimbidwa kumapeto kwa msewu, kumene pokhota papakulu apa padzachotsedwa. Kuli Winawake kumeneko amene akukoka pamtima panu, akudziwa kuti tsiku lina mudzakwezedwa mmwamba. Ngati zimenezo sizinachoke pa mtima panu lero, mzanga, mzika imzanga, mwendamnjira. . .

¹⁵⁴ Kagulu, kapang’ono kusauka, Mulungu adalitse mtima wanu. Ndikukuwonani inu mutakhala apa, muli ndi tsitsi

laimvi ndi mapewa-akugwa. Kuwona ana osawuka, aang'ono, amene mwinamwake amayenera kuphonya zakudya. Ndipo kodi ine ndingayime pano ndikunena chirichonse cholakwika kwa inu? Zimenezo, chabwino, Mulungu asalole! Ndingakhale a . . . Ine ndikuyenera ndifike mmusi ndi kudzalapa ndisanalalikire nkomwe. Ine ndimakukondani inu. Ndipo zimenezo ndi chikondi chenicheni cha Chikristu.

155 Mukhale woona mtima tsopano ndi Mzimu Woyera. Kodi zinthu zonsezo zachoka kwa inu? Kapena, kodi Satana wakunyengani inu, ndipo mukungokhala moyo wa theka chabe? Nthawizina mumaganiza, “Chabwino, ziri bwino,” ndipo nthawi ina, bwanji, inu, “Chabwino, ine sindikudziwa”? Ndipo zinthu zimachitika, zimene inu mukudziwa. Ndipo ngati ndicho chikhaliidwe chanu, ndipo mmawa uno, mukufuna kupereka zonsezo kwa Khristu.

156 Kumbukirani zimene Iye ananena. “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo, pakali pano, Moyo wosatha.” Chiweruzo chatha. Kuyambira nthawi imeneyo, chinthucho chikhala chakufa. Ngati inu mukuvomereza izo kwenikweni, izo zizitsimikizira zokha.

157 Tsopano taonani. Musanyengedwe. Inu mukukumbukira kuno, zaka zapitazo pamene ife tinali ndi mpingo mu dongosolo? Ine ndikuyankhula ndi inu, ndipo inu mukupemphera; mitu yoweramitsidwa. Mukukumbukira pamene ife tinali ndi mpingo mu dongosolo? Pamene uthenga uperekedwa mwa uneneri, kapena mmalirime ndi kutanthauzira, pamene tinkalemba izo ndi kuziyika izo pano pa nsanja, kuchitiridwa umboni ndi amuna atatu. Ine ndimapereka uthenga kuchokera pa nsanja. Ngati izo sizichitika, inu munali ndi mzimu woyipa pakati panu. Inu mubwere kuno ndi kudzakonza izo.

158 Ngati munthu wachita chimene chinali cholakwika, mlongo kapena m'bale nkuwawona iwo akuchita zolakwa, iwo ankapita kwa iwo. Pamene iwo akubwera ku tchalitchi, ankawagwira iwo pa nkono, amapita kuseri mchipinda chaching'ono, nkukati, “M'bale, ine ndinakuwonani inu pa malo olakwika. Ine sindizina izo pamaso pa mpingo, chifukwa ine ndimakukondani inu. Inu munalakwitsa. Tiyeni tipemphere tsopano.” Mukuona?

159 Tsopano mukhale owonamtima ndi inueni. Ngati chikondi cha Khristu chiri mumtima mwanu, kuposa chirichonse, Mulungu akudalitseni inu; muli bwino. Koma ngati sichoncho, musanyengedwe. Mizimu imeneyo ndi yachinyengo momwe ingakhali. Iyo imakunyengani inu. Izi ndi zomwe anachita kwa Eva, anamuwuzwa iye zochuluka za choona chatsopano. “Oh, inde, Mulungu wanena. Uh-huh.” Koma pali cholakwika pang'ono mmenemo. Ndi zimene . . . Ndi zimene zatiphwanya ife

mmawa uno; ife timawona cholakwika chaching’ono mu unyolo. Ndi chimene chimapangitsa mavuto onsewo.

¹⁶⁰ M’bale, ngati sizikuyenda bwino ndi mtima wa Mulungu, kodi mungakwezere dzanja lanu tsopano kwa Mulungu, ndikuti, “Mulungu, ndi ichi, ine ndikufuna kwenikweni kuti ndikhale wolondola?” Aliyense asayang’ane kupatula ine. Kwezani mmwamba dzanja lanu. Mulungu akudalitse iwe, dona. Winawakenso? Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, ndi inu, ndi inu, ndi inu, inu. Mulungu akudalitseni inu. Tsopano, Iye amakudziwani inu. Amamudziwa aliyense wa inu. Iye amadziwa basi chomwe inu mukufuna.

¹⁶¹ Tsopano, kachitidwe kathu kachikale (pamene inu mwaweramitsa mutu wanu) ndi kuti anthu abwere ku guwa. Izo ziri bwino. Ine ndikuzikonda zimenezo. Imeneyo si nkhani ya m’Baibulo. Icho ndi chiphunzitso chabe cha mpingo.

¹⁶² “Onse amene anamulandira Iye, kwa iwo Iye anawapatsa mphanvu yokhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu.” Pomwepo pamene mwakhalapo, ndipo mwakweza dzanja lanu, dazeni kapena kuposerapo a inu pano, kodi inu mungavomereze tsopano, pansu pa mtima wanu, mutatha kunena kuti mukumverera kuti mukuyenera kutero? Kodi inu, gulu lomwe lija amene munakweza dzanja lanu, mungakweze dzanja lanu, ndikuti, “Ine tsopano ndivomereza izi, M’bale Branham. Ine tsopano ndimulandira Yesu. Ziribe kanthu kuti ndinachita chiyani, ine tsopano ndikumulandira Iye ngati Wokondana naye wanga ndi Mpulumutsi wanga?” Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, dona. “Ine tsopano ndimuvomereza Iye. Chinachake mu mtima mwanga chikundiiza ine kuti ine—ine—ine ndikufuna kutero. Pali Chinachake chikundiiza ine kuti ndikuyenera kutero, pakali pano. Ili ndi tsiku langa. Mwinamwake nthawi yotsatira, ndidzakhala kutali kwambiri.” Mulungu akudalitseni inu, bambo. Mulungu akudalitseni inu, m’bale. Mulungu akudalitseni inu, dona. Ine ndikuwona dzanja lanu. “Tsopano ndikumverera kuti ndikuyenera ndichite zimenezo.”

¹⁶³ Amzanga, mpingo ukuzizira. Amerika aweruzidwa posachedwapa. Fuko lililonse linalandira izo. Kodi inu mudzakhala chiyani zaka handiredi kuchokera pano? Mudzakhala kwinakwake. Nthawiina pakati pa miniti ino ndi zaka handiredi kuyambira tsopano, inu mukuchoka mdziko lino. Inu zikanakhala bwino mukanakhala otsimikiza. Osasewera nazo izo. Mawu akulalikidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo Iwo ndi Choonadi chochokera ku Mawu a Mulungu. Pali Winawake amene amakukondani inu.

¹⁶⁴ Tsopano, inu simungakweze dzanja lanu, pokhapokha Winawake atakuitanani kuti mukweze dzanja lanu. Ameneyo

ndi Mzimu Woyera. “Palibe munthu angadze kwa Ine, kupatula Atate Anga atamukoka iye poyamba.” Ndipo ngati Iye amakukondani inu mokwanira kuti agogode pa mtima wanu, ndikuti, “Inde, ndikutanthauza iwe. Nthawi yake ndi inoyi. Ine ndikufuna kuti ndilowe mkati, Ine ndisanakuchotseni pa dziko lapansi nthawi isanakwane. Ine tsopano ndikufunsani inu kuti mukweze dzanja lanu.” Kodi inu simuchita zimenezo ndiye?

¹⁶⁵ Winanso wowonjezera akuti, “Ine tsopano, kuchokera pansu pa solo yanga, ndikuvomereza izo”? Tsopano ine ndikupemphererani inu. Mulungu akudalitseni inu, dona. Ine ndimangomverera, mlongo wokonedwa, uyo anali inu. Ine ndinayang’ana mmbuyo uko... Ndithudi, inu nonse mukuzindikira kuti ndatsala ndi masiku ochepa, maora pang’ono, msonkhano usanachitike kutsidyako. Ine ndikukhala mchipinda changa mochuluka tsopano, kumapemphera. Msonkhano wamachiritso; Mngelo wa Ambuye ali pafupi. Zinthu zazikulu zichitika. Ine ndinayang’ana mmbuyo ndipo ndinawona Chinachake chitayima mchipinda, Icho chinali pa mkazi wamng’ono. Ine ndinawawona ena akukweza dzanja lawo. Ndinamverera umboni kuti izo zinali zoono. Ine ndinaganiza, “Ngati ine ndingapange kuyitana kwina kumodzi, ngati mkazi ameneyo angakweze dzanja lake.” Ndipo iye anatero. Zinali chomwecho.

¹⁶⁶ Tsopano, Mulungu, Wokonda solo yathu, ife ndi ndani, mulimonse? Bwanji, dziko lisanapangidwe nkomwe, Inu munadziwa udzudzu uliwonse ukanadzakhala pa dziko lapansi, nyererere iliyonse, nthata iliyonse. Inu ndinu wopandamalire. Ndipo Inu mumadziwa izo, mmawa uno, kuti anthu adzakweza dzanja lawo. Inu mumazidziwa izo. Bwanji, Inu munawawona iwo dziko lisanayambe. Inu mumazidziwa izo, nthawizonse. Ndipo Inu mumadziwa kuti chinthu ichi chikanadzachitika, kuti Inu mukhoza kufotokoza chikondi Chanu kwa anthu Anu. Inu munati munamuukitsa Farao ndi kuwumitsa mtima wake, kuti Inu mukathe kuwonetsa mphamvu Yanu, koposa kotani kuti Muwonetsere chikondi Chanu! Satana, woyipayo amene anapotoza chabwino kukhala choyipa, Inu munamulola iye achite zimenezo, chifukwa Inu mukhoza kufotokoza chikondi Chanu ndiye kwa anthu Anu. Ndipo, O Mulungu, ife timakukondani Inu kwambiri! Ife timakuyamikirani Inu.

¹⁶⁷ Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, kuti anthu awa akhale moyo wa Chikhristu, wodzichepetsa, kuyambira lero kupita mtsogolo, monga iwo akuvomerezani Inu. Ndipo ngati alipo ena, mwinamwake sindinawawonepo iwo onse, mwinamwake Inu simunawawonetsere iwo kwa ine, koma Inu mwayankhula nawo iwo. Ngati alipo ena, adalitseni iwo nawonso. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Pali Kasupe wodzazidwa ndi Magazi,
 Kuchokera ku mitsempha ya Emmanuele,
 Ndipo ochimwa akadziponyera pansu pa
 kusefukirako,
 Ataya mlandu wawo wonse...
 (Pang'onopang'ono tsopano, mlongo.)

¹⁶⁸ Inu mukudziwa, dzulo, M'bale Roberson anali kwa M'bale Wood. Ine ndinazembera kumusi. Ine ndinali kudikirira mtumiki wina wodzatiyendera kuti abwere. Iye anaponyera chithunzi, ndipo chithunzicho chinali...Zambiri za izo tinali kuziyang'ana, koma, chimodzi cha izo, pamene mpingo umayenda kutuluka pakhomo. Ndipo ine ndinadziwona ndekha ndikutuluka panja apo, ndipo ine ndinayang'ana, "Oh, mai! Mnyamata, bwanji, chimene zaka zochepa zakupangira iwe!" Ndipo ine ndinayang'ananso. Izo zinabwera mmalingaliro anga, mmawa uno.

¹⁶⁹ Basi masiku pang'ono ena chabe amene ife tiri nawo a zovuta izi ndi machimo. Ndipo ine ndikuganiza za nthawi zimene ndinamva nyimbo imeneyo ikuyamba, kuwawona iwo akupita panjira yawo apa, atayima mozungulira guwa kuti adye mgonero. Ndipo ndamvapo matayala a bokosi akulira, pamene ankatsikira mchipinda mmenemo, akuwatulutsa iwo.

¹⁷⁰ Kumbukirani, kulalikirira kwa Mawu awa kudzakhala a... Kudzaima pa Chiweruzo. Ndipo ine ndidzayenera kudzaima kumbuyo kwa Iwo, kudzaima pamene. Ine ndiyenera ndidzakhale mboni ya zimenezo. Ine sindingathe kuwabweza Iwo. Ine ndawanena kale Iwo. Ine ndiyenera kuti ndikhale ndi zimenezo. Iwo adzakakumana nane ine mu Chiweruzo, chimodzimidzi monga momwe Mulungu ananenera Mawu Ake ndipo sangathe kuwabweza Iwo. Mukuona?

¹⁷¹ Ndipo ine ndimawayeza mawu aliwonse, poyamba mu mtima mwanga, ndi kuwona ngati ine ndikufuna kuwanena iwo, inemwini. Ngati akuwoneka olakwika, ine sindimawanena iwo. Ine ndimamulola Iye anene izo. Ngati-ngati Iye anena chinachake, mosiyana, ngakhale ine nditati ndisakhulupirire izo, ine ndinganene izo, mulimonse, chifukwa ndi Iyeyo. Ine ndimafuna kukhala wotsimikiza, chifukwa sindikufuna zolakwitsa zirizonse tsiku limenelo.

¹⁷² Inu mukudziwa, kudzakhala kwa mdima kwambiri, kumusi pa mtsinje, tsiku limenelo. Sikudzakhala aliyense woti adzathandize. Inu simudzapita ndi ndalama kumusi kumeneko. Azimzanu adzakhala chimodzimidzi momwe inu muliri; kudzakhala mdima wowopsya. Inu mudzayenera kuti mudzawoloke. Ine ndikufuna ndidzakhale wotsimikiza kuti tikiti yanga ndi yolondola. Ine ndikufuna ndidzakhale wotsimikiza, pamene ndizidzayang'ana pa iyo, ndizidzawona Magazi ofiira a Mbuye wanga. Ndiye pamene ndidzamva,

patapita kanthawi, Chombo chakale chikuwombedwa, zidzakhala bwino ndiye. Koma sindikufuna vuto lililonse kumusi kumeneko. Ine ndikufuna ndizikonze izo tsopano. Ngati pali vuto lililonse, ndikufuna kuti likonzedwe tsopano. Ine ndidzasowa chidutswa chirichonse cha chisomo chimene ndingadzachipeze, pa tsiku limenelo.

¹⁷³ Ine ndidzakhala woonamtima. Monga mphunzitsi wamkulu ananena, tsiku lina, iye sanafune kukhala wotchuka, iye ankafuna kukhala woonamtima. Ine ndikufuula langa limodzi naye. Ine ndikufuna kukhala woonamtima. Ine ndikufuna kunena Choonadi, chotero pa tsiku limenelo, pamene idzafika, ndidzamva kufuula kuzungulira pa gombe, ndikufuna ndizidzayang'ana pansu ndi kukhala wotsimikiza.

¹⁷⁴ Monga ana Achihebri, pamene iwo anawona mapiko akuda amenewo akubwera, a imfa, mnyamata wamng'onoyo anati kwa abambo, “Kodi inu mukutsimikiza kuti magari ali pa mphuthu?”

Abambo amakayang'ana pamenepo, “Eya, mwana, magari ali pamenepo.”

“Chabwino, ndiye ziri bwino zikatero. Ndife otetezeka.”

Iwo palibepo, mmawa uno, mzanga?

Khalani otsimikiza.

¹⁷⁵ Tsopano, Ora May, ine ndikudziwa inu mwabwera kuti mudzapemphereredwe, mlongo. Mtsikana wamng'ono wosauka uyu, momwe iye ankakhalira apa pa mzere, ngati kanthu kakang'ono pamenepo. Shirley wamng'ono wakhala apayu, akulira, wangobwera kumene kuchokera ku Arizona. Ine ndimaganiza za ana aang'ono amenewo. Nonse a inu mukuwakumbukira iwo, kunja kuno mu yaing'ono—nyumba yaing'ono ya bokosi yakale, abambo awo okalamba osauka atakhala limodzi kuseri kwa tchalitchi kuno, kwa iwo. Mukukumbukira, anyamata aang'ono amenewo momwe ine . . . momwe tonse timawadziwira iwo. Momwe Ora May wosauka wamng'ono . . . Zimatengera awiri kuti alere banja. O Mulungu, chinthu choyipa ichi cha chikwati ndi chilekano. Ndi momwe Curtiu anachitira chopambana chimene iye akanatha, mwa iwo. Anagwira ntchito molimbika. Koma, mwana, mosasamala kuti ndi ndani, amafunikira chikondi cha amayi. Winawake woti aziwakonda iwo. Ndi chirengedwe, choti chizitonholetsa kumverera kwako.

¹⁷⁶ Ndine wosaka. Ine ndimayang'ana moyo wazinyama za mtchire. Ndizo basi . . . Ndipo ine ndimapitako ndi kukaziphunzira izo. Chimbalangondo chachikazi chokalamba, pamene icho chilowa, mu kugwa masamba kwa chaka, chimabadwa kuti chikhale mayi kenanso. Chimawathamangitsa ana ake onse. Icho chimakhala ndi mmodzi mpaka awiri; icho

chimawathamangitsa iwo, kuwapanga iwo kuti akagone okha, kuti iwo azolowere izo.

¹⁷⁷ Chaka chotsatira, pamene icho chikutuluka, icho chimakhala ndi ana ena awiri aang'ono, mmodzi kapena awiri owonjezera. Icho chimawayamwitsa iwo kudutsa mu chirimwe. Ndiye, mkugwa kwa masamba, icho chimawathamangitsira iwo kutali.

¹⁷⁸ Icho chimadzakhala ndi awiri ena chirimwe chotsatira. Koma nanga bwanji ngati sichikhala ndi ana chaka chimenecho? Inu mukudziwa chimene icho chimachita? Chimatuluka, chimayesetsa kukapeza ana amenewo, iwo amakhala kuti akula monga momwe icho chiliri. Ngati icho sichingawapeze iwo, icho chimakatenga mimbulu yaying'ono ingapo. Icho chimakatenga agalu angapo. Icho chimakatenga, kwenikweni, mwana wamunthu. Ndithudi, izo zinachitikapo. Icho chimakamutenga mwana wamng'ono ameneyo, kapena chirichonse, ndipo icho chimamuyamwitsa iye. Ndi chirengedwe basi. Icho sichingachitire mwina.

¹⁷⁹ Tamuwonani mtsikana wamng'ono ndi chidole chake, bwanji, iye sali usinkhu wa zaka zitatu. Ine ndinamuwona Sarah wanga wamng'ono, usiku wina. Ine ndinalowa mchipinda. Kanthu kakang'ono kamanjenje, ndipo apo iye anali, atagona ndi kachidole kake kakang'ono pa dzanja lake. Ine ndinaima pamenepo ndipo ndinayang'ana pansi. Ine ndinaganiza, "Kanthu kakang'ono kosauka! Inu mukudziwa, sizikhala motalika, zaka zambiri, abambo adzakalamba, pakapita kanthawi. Ine ndine tsopano; wa imvi ndipo ndadutsa." Koma kumeneko ndi kuchita mthunzi, tsiku lina, a—weniweni, mwana wamng'ono wagona apoyo. Zimangokhala mwa iwe. Ndipo ngati iwe sukuwakonda anyamata aang'ono amenewo, chinachake chidzatenga malo ake.

¹⁸⁰ Ngati munthu samupembedza Mulungu, iye adzapembedza galimoto yake, iye adzapita ku bala, iye—iye adzapanga chinachake, iye azidzathamanga uku ndi uku. Chifukwa, pali chinachake chimene chikuyenera kuti chitenge malo amenewo.

¹⁸¹ Tsopano, mlongo wathu, sindikutanthauza kuti ndikhale. . . ndimupangitse iye atengeke. Koma, posakhala ndi chisamaliro cha amayi, molondola, chinachake chinatenga malo ake. Ndipo kanthu kakang'ono kosauka kakuvutika, mmawa uno, chifukwa cha manjenje; ana awiri aang'ono. Iye analakwitsapo; chimodzimidzinso monga ndi ine, ndipo ndi ndani winanso amene sanatero? Koma ine ndikuyesera kunena kuti, pali Winawake amene anakhululukira izo. Iye anakweza dzanja lake kanthawi kapitako; zonse zapita. Zimenezo zinachokera mumtima woota, chimene ine ndikufuna kukhulupirira kuti zinatero; mungoona chimene chiti chichitike. Pamene iye

adzakhala mkazi wokalama wa imvi, izo zidzaimabe. Uko nkulondola. Koma, iye akuchita manjenje.

¹⁸² Palibe mankhwala padziko lapansi omwe angathandize mitsempha. Ngati mungamwe mankhwala, kuti mukhazikitse mitsempha yanu, iwo adzakupangitsani inu kukhala woyipa pawiri iwo akadzakusiyani inu.

¹⁸³ Palibepo mankhwala a manjenje, koma ndine wokondwa kwambiri kuti pali machiritso. Inu mukudziwa, ine ndavutikapo ndi izo, nanenso. Alipo machiritso, osati mankhwala; machiritso, kuchiritsa kawiri!

¹⁸⁴ Pa ulaliki wanga dzulo, pa wailesi: *Muvi Wa Chiwombolo*. Alaliki amamenya pang'ono za izo, monga anachitira Joashi. Iye bwenzi atamenya mowonjezera.

Koma, penyani, m'bale wanga, mlongo. Mankhwalawo ndi Khristu.

¹⁸⁵ Kapena, mulole ine ndinene ichi, pa guwa, kuseri kwa bokosi laling'ono lakale ili linamangidwa pano; koma ilo ndi lopatulika monga guwa lirilonse la Uthenga. Ilo linaperekedwa kwa Mulungu. Ndife anthu osauka. Mwinamwake ilo liribe golide pamwamba, koma Mzimu Woyera wabwera kuno ndipo watichitira ife zinthu zazikulu.

¹⁸⁶ Mlongo wanga, wokondedwa, Mulungu adalitse mtima wako waung'ono. Monga mayi, komanso ngati mwana, ngati mungavomereze zomwe M'bale Bill wanena...kapena akukuuzani inu tsopano, Ine ndikukutsimikizirani inu, wokondedwa, kuti muzichoka pano, mukakhala bwino bwino.

¹⁸⁷ Tsopano, pamene inu munakweza dzanja lanu kanthawi kapitako, nthawi imeneyo inu munamuvomereza Khristu. Ine ndikufuna inu, mu maminiti pang'ono, ine ndikufuna kuti inu mubwere kuno. Ndipo ine ndikhoza kutsimikizira kwa inu, mwa...Inu, mukhale woweruza. Mwa chisomo cha Mulungu, ndi Mzimu Woyera umene wayima pano, ine ndikhoza kupangitsa izo kuti zikusiyeni inu. Uko nkulondola. Ine sindinayambe ndaziwonapo izo zikulephera. Komano izo zidzabwerera kwa inu mukachoka pano, mwaona, ngati mungazilole izo. Koma ngati simuzilandiranso izo, ziribe kanthu kuti mukumverera chotani; inu muzipita mukuti, "Yesu Khristu wandichiza ine."

¹⁸⁸ Onani, inu mwatsika, Ora May, kuchokera pamwamba *apa*, pamene inu munkakonda kukhala wokondwa ndi kumakwera njinga imeneyo, ndi kumathamanga chokwera ndi chotsika mu msewu kuno. Inu munkakhala okondwa nthawi imeneyo. Inu simumakhala ndi kumverera kumene inu muli nako pano, sichoncho inu? Mukuona? Tsopano inu mwatsikira pansu *apa*, ndi chifukwa chakuti panalibe chirichonse choti chikugwireni, wokondedwa. Inu mwagwera pansu *apa*. Koma tsopano inu mukuyenera kukhulupirira kuti mwafika *apa*, ndipo

mukhulupirire izo. “Ndipo chikhulupiriro chopanda ntchito ndi chakufa.” Ngati ukukhulupirira izo, ndiye uchite ngati uli pamwamba pamenepo, ndiyeno Mulungu adzangokukwezera iwe pamwamba pamenepo kenanso.

¹⁸⁹ Apo pali Adzakhali ako Meda akhala kumbuyo uko. Iwo anali ndi chinthu chomwecho. Ine ndinali ndi chinthu chomwecho. Ine ndikudziwa chimene icho chiri, koma Mulungu ndiye machiritso.

Kodi iwe ukhulupirira izo, mmawa uno, Ora May?

¹⁹⁰ Ine ndikufuna iwe ubwere kuno. Aliyense wa inu nonse, mukudwala, kuti mudzodzedwe. Chabwino.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi chabe.

¹⁹¹ Mpingo, nonse inu mukumudziwa Curtis. Mukumudziwa Ora May. Kungomuyang’ana Ora May, mukhoza kuwona kuti chinachake chachitika. Iye watopa ndipo wakhumudwa. Ora May, ino ndi nthawi yokhazikika.

¹⁹² Ine ndikufuna ndikufunse iwe chinachake. Nthawi zambiri, Ora May, wanenapo kuti, “Ngati ine ndikanangopeza malo oti ndiyambirepo. Ngati ine ndikanangoyambira nthawi ino kumamverera bwino, ndikukhulupirira nditha kudzithandiza ndekha kuti ndituluke muno.” Mwaona, uko nkulondola, sichoncho izo? Chabwino, iwe uli pamalopo tsopano, Ora May. Iwe uli pamalo abwino kwambiri padziko lapansi, pa guwa, pamene Munthu yekhayo padziko lapansi angakuthandize, kutero, ndi Mulungu.

¹⁹³ Ine ndikufuna kuti muweramitse mitu yanu, aliyense, mulumikizane ndi ine mu pemphero.

¹⁹⁴ Wokonedwa Atate Akumwamba, monga mtsikana wamng’ono wosauka uyu... Moyo ndi waufupi kwambiri. Tsopano iye ndi mayi wachichepere. Ine ndikudziwa, kanthawi kapitako, pamene iye anakweza dzanja lake, tchimo lililonse linachotsedwapo. Mulungu, Baibulo Lanu ndi mboni ya izo. Inu munayankhula Iwo kuchokera Kumwamba, kuti, “Iye amene ati adzakhulupirire, adzalandira.”

¹⁹⁵ Tsopano, iye ali ndi kulimbana kowopsya patsogolo pake, Ambuye. Ndipo Satana amakhoza kumuponjera iye, kutsidyako, ndi kuwalanda ana amenewo kwa iye, ndi kukamuika iye ku chipatala cha amisala, kuti adzikamenyetsa mitu wake kukhoma. Koma iye wabwera ku malo oyenera, lero, pa guwa. Iye wabwera ku nyumba ya Mulungu wamoyo. Iye wayima pano, monga zinachitikira, yekha, paguwa, koma osati yekha. Angelo a Mulungu amuzungulira. Mzimu Woyera uli pafupi, nawonso. Ndipo iye ndi mboni ya kuwona zinthu zambiri zikuchitika, ndikudziwa kuti Inu ndi Mulungu. Ndipo ine ndikupemphera kuti, ndi mtima wanga wonse, ndi solo yanga yonse, kuti, lero, kuti Inu mumuthandize Ora May.

¹⁹⁶ Tsopano, Atate, ndikutenga kuchokera paguwa lino, chimene chakhala pano pa malo opatulika awa pamene Mzimu Woyera waphimba . . . Iwo amatchedwa mafuta a azitona, kapena mafuta odzozedwa, mafuta odzozera. Izo ndi mogwirizana ndi zomwe Munanena, mafuta ochokera ku azitona wa nthambi. Ndipo tsopano pamene ine ndikupita patsogolo kukamudzoza mlongo wanga ndi mafuta awa, Inu munati, “Pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa odwala.” Nditatha kulalikira Uthenga . . .

¹⁹⁷ Podziwa kuti ntchito yayikulu iyi ikubwera, kufuna Kwanu kuchitike, kuno ku Indianapolis, kumene amisala ambiri, ogontha, osayankhula, akhungu, ndi chirichonse, adzaima pamene. Koma ife sitikuwopa chidutswa chimodzi. Inu munayankhula izo, dziko lisanayambe. Ife tiri nako kukhudza kwa Kumwamba, kumeneko, kumene kumatiuza ife kuti ndi Choonadi. Ife tikupita patsogolo ndiye kukamutsutsa mdierekezi ameneyo. Anthu athu ali pamavuto, chimodzimidzi monga Loti anali, mu ulaliki mmawa uno, ndipo Abrahamu anamutsatira iye.

¹⁹⁸ Satana, ife tikukutsatira iwe, mmawa uno. Mlongo wathu wosauka, wamng’ono wosiyidwa ali pamavuto, ndipo ife tikukutsatira iwe. Ndi mafuta odzozedwa, ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi Mawu Auzimu a Mulungu, ndi Uthenga, ife tikupita kukayika manja pa iye, mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo ife tikukuthamangitsa iwe uchoke kwa iye. Yesu anati, “Pitani,” ndipo sangalephere; anati, “Mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda.” Ndipo ndiwe mdierekezi. Pomvera lamulo Lake, tikukutulutsira iwe kutali ndi uyu, wamng’ono wanga . . . ife tikupembedzera tsopano, kuwoneka ngati wosiyidwa. Magazi a Yesu Khristu amutsuka iye ku tchimo lonse. Lero iye wakhala wangwiro ndi woyera pamaso pa Mulungu, mwa kuvomereza kwa tchimo lake, mwa kuyeretsa kwa Uthenga. Ife tikuzitulutsa izo, manjenje awa. Oh, inde, iwe umamuitana iye, koma sungakhoze kumugwira iye. Ife tikuchonderera Magazi pakati pa iye ndi uyu. Iwo akuyima ngati mkhalapakati. Ndipo tsopano iwe umusiye mtsikanayu. Umusiye iye azipita mfulu. Ndipo kuyambira lero, umulole iye akhale wokondwa. Chifukwa cha ana aang’ono awo agona apowo.

¹⁹⁹ Chifukwa, cha mwamuna uyo, mulole nayenso abwere ndi kudzakhala Mkhristu. Mulole zonse zake, ndipo tsiku lina mu Ulemerero, mkombero wa banja waukulu udzakhale wosasweka kutsidyako. Mulole amayi ake, abambo ake, zake zonse, aliyense, adzakhale Kumeneko. O Mulungu, perekani izi.

²⁰⁰ Mulole iye akhale womasuka kuyambira ora lino. Ife tikumumasula iye, ndi chikondi changwiro, ndi kulamula izi kudzera mu Baibulo; ndi imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiwukitsiro cha Yesu Khristu; kudzera mu Magazi Ake ndi

Mzimu Woyera. Ife tikumubweretsa iye kwa Inu, kudzera mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

²⁰¹ Chabwino, pita tsopano. Zinthu zibwerera mwakale. Iwe ukumverera bwino tsopano? Osati kukupweteka tsopano; umverera bwino tsopano.

²⁰² [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. . . uzikhala chomwechi nthawi zonse, zikhala bwino. Ndithudi. Amen. Tsopano zatha, mlongo. Izi zikukupangitsa iwe kumverera mpumulo? Tsopano utha kuchoka pano, kazituluka, ukakhale Ora May kachiwiri, kokha, Ora May watsopano, mtsikana wokondwa mwa Khristu. Ulole izo zonse zipite. Udzabwerere kuno, pafupifupi chaka kuchokera lero, Mulungu akalola; udzabwere, ndikuti, “M’bale Branham, mukukumbukira mmawa umene inu munandipempherera ine uko pa guwa? Izo zinakhazikitsa izo.” Mulungu akudalitse iwe. Ambuye alemekezeke.

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu tsopano.

²⁰³ Atate wathu Akumwamba, pomvera lamulo la Ambuye ndi Mpulumutsi wathu, Yesu Khristu, ife tikukukondani Inu lero, ndi chikondi changwiro, choyera, chosasakanizidwa. Ndipo mulole chifundo Chanu ndi chifundo zikhale pa wina aliyense. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha alendo omwe ali pachipata chathu. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mumudalitse aliyense.

²⁰⁴ Mdalitseni m’busa wathu wokondedwa, M’bale Neville wathu, amene amayima ndi ife mu kulumikizana kwa Uthenga; osati womangika goli ndi dziko lapansi, koma womangirizidwa pamodzi ndi Khristu; zingwe zonse za Mulungu kupitirirabe, kumakoka galeta lakale la Uthenga, mopitirira, omangidwa pamodzi monga mzika zimzathu ndi atumiki a Mulungu.

²⁰⁵ Adalitseni madikoni onse, trastii, msungichuma, aliyense amene akukhudzidwa, mamembala onse, anthu wamba, alendo. Mulungu, kukubwera msonkhano kutsidya ku Indianapolis. Mulungu, sindine woyenera kudalitsidwa, koma kodhi Inu mungawadalitse anthuwa, kudzera mu kulalikira kwa Mawu! Mosakayikira koma mahandirede ayima.

²⁰⁶ Tikumudzozanso dona uyu, mu Dzina la Yesu Khristu, kuti Inu mumuthandize iye ndi kuchotsa vuto lake, pamene ife tikuika manja pa iye, kudzera mu Dzina la Yesu Khristu. Tsopano, Atate Akumwamba, perekani kuti chifundo Chanu chiwonjezedwe kwa iye, mu Dzina la Khristu.

²⁰⁷ Tsopano ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ndikudabwa tsopano ngati pali wina aliyense pano amene anga—angabwere pa guwa, angafune kubwera ndi kudzagwada pa Mawu a pemphero, amene wamuvomera Khristu, kapena akumverera ngati kuti angakonde kupemphera pang’ono kutatha kuchezero

kwa Mzimu Woyera. Kodi inu simukumverera bwino kwenikweni za izi? Simukumva bwino?

Bwerani kuno, M'bale Neville.

²⁰⁸ Ndi angati angakweze dzanja lanu, ndikuti, “Ndikufuna kuti ndibwere ku guwa ku pempherepo pang’ono chabe.” Kodi mungakweze dzanja lanu, ndikuti, “Ndikungofuna kuti ndiziyeretse ndekha, pang’ono.” Oh, Mulungu akudalitseni inu. Chabwino.

²⁰⁹ Tsopano, mwaona, M'bale wathu Neville, ine ndikuganiza, ine ndamuzindikira iye mu mayendedwe ake onse, iye wakhala ali mwamuna weniweni. Ndimamupeza iye yemweyo tsiku lililonse. Kaya nkondo ikuyenda bwino kapena ayi, M'bale Neville samasintha. Ine ndikuthokoza Mulungu chifukwa cha izo. M'bale Neville sangakhoze kuchita izo mwa iye yekha; zimatengera Mulungu kuti achite izo. Ndipo ndine wokondwa kuti gulu ili la nkhoa liri ndi m'busa ngati M'bale Neville. Ine ndikupemphera kuti Mzimu Woyera umuthandize iye ndi kumudalitsa iye. Ine ndimamukonda iye. Ndipo ine ndimawakonda anthu Ake. Ndipo anthu nonsenu timakukondani, ndipo ife tikupemphera kuti Mulungu akudalitseni inu.

²¹⁰ Koma tsopano pamene ife tikuweramitsanso mitu yathu, ine ndifunsa kuti iwo amene angafune kuti apemphereredwe, ndipo akufuna kuti agwade ndi kudziyeretsa nokha, abwere modzichepetsa pa guwa.

²¹¹ Tsopano, M'bale Neville, inu muwapempherere iwo, ngati inu mungathe. Ndikufuna inu mukhale pa izi. Aliyense akupemphera.

[M'bale Neville akupemphera—Mkonzi].

Ngati inu mungabwere pa gu- . . .



UNGIWIRO CHA56-0610
(Perfection)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu mmawa, Juni 10, 1956, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2022 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org